

KODI NDINGAGONJETSE BWANJI?



Tiyeni tiweramitse mitu yathu kwa pemphero.

Atate athu, ife tikukuthokozani Inu, mmawa uno, chifukwa cha nthawi yopambana iyi ya kubwera pamodzi kanonso, ndi kudzatsegula Mawu a Ambuye, Iwo ali patsogolo pathu. Ndipo—ndi pemphero tsopano, kuti Mzimu Woyera utenge icho chimene chiri Mulungu, ndipo uchipereke Icho kwa ife, kuti ife tikathe kuchoka pamalo ano opembedzerapo lero ndi mitima yokondwa yodzaza ndi chimwemwe. Kuwona mphamvu Yanu yaikulu ya chiwombolo, Ambuye, mmene iyo imamuwombolera wa nsinga ndi kuwapanga iwo amfulu, kutidziwitsa ife “zinthu zimene zinaliko, ndi zomwe ziripo, ndi zomwe ziri nkudza.” Ndipo ife tikungokuthokozani Inu chifukwa cha zinthu izi.

² Ife tikupemphera kuti Inu mutidalitse ife pamene ife tikuwerenga Mawu Anu tsopano limodzi. Ndipo pamene ife tidzichoka, mulole chikanenedwe m’mitima mwathu, pamene ife tizipita tikuyenda mnjirayi, “Mitima yathu inatentha mkati mwathu pamene Iye, Mzimu Woyera, amalankhula nafe pamene ife tinali panjira.”

³ Mudalitse mtumiki aliyense lero, konsekonse, antchito Anu amene akuimira Ichi, Choonadi Chanu. Muyankhe mapemphero awo a kwa odwala. Muchize matupi odwala a iwo amene akudwala.

⁴ Ambuye, ife tikupempha kuti Inu mupite kunja pakati pa anthu ndipo mukafunefune mbewu yokonzedweratu iyo uko, Ambuye, ndipo muibweretse iyo, mwanjira inayake, kuti Kuwala kukagwere pa njirayo, Ambuye. Pakuti, ife tikukhulupirira kuti ora likupita kumapeto, dzuwa mwaliwiro likukalowa kumadzulo, ndiye posachedwapa zidzakhala kuti “nthawi siidzakhalaonso.” Nthawi ndi Muyaya zidzalumikizana limodzi pamene Mulungu ndi anthu Ake ati adzalumikizane pamodzi. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti, pa nthawi imeneyo, kuti ife tidzawerengeredwa limodzi ndi iwo amene adzalumikizidwe mwa Khristu, amene akutchedwa Mkwatibwi Wake.

Mutithandize ife, lero, pamene ife tikukonzekera, mosadziwa chimene mawa liti lisungire, koma ife takonzekera kuti tilandire chirichonse, Ambuye, monga mmene ife tikudziwira, chimene Inu mwatisungira ife. Ife tiri okonzeka kulandira Icho. Ife tikupempha mdalitso uwu kwa ulemelero wa Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Inu mukhoza kukhala pansu.

⁵ Ine ndithudi ndinali wokondwa, mmawa uno, pamene ine ndimalowa ndi kuwona kuti a—anthu asonkhanira pamodzi

utumiki wa Ambuye. Ndipo ife tikulengeza tsopano kwa usikuuno. Tikhala ndi utumiki wa machiritso usikuuno. Ife tidzakhala tikupempherera odwala, usikuuno. Mphindi pang'ono chabe zapitazo, iwo. . .

⁶ Pamene ine ndimabwera, Billy, mwana wanga, amandiuza ine, anati, “Pali—njonda pano, iye ndi bambo wosauka basi amene wayendetsa mtunda wautali.” Ndipo anati, “Ine—ine ndamuika iye mchipinda, Adadi.”

⁷ Ine—ine ndinafika mochedwa usiku watha, ndipo—ndipo sindinakwanitse kuti ndiwerenge mokwanira pa phunziro la Sande sukulu limene ine ndimati ndiyankhulepo, mmawa uno. Kotero ine ndinatenga zolemba zina zapang'ono zomwe ine ndinatenga kuchokera ku chimene ine ndinamumva m'bale wina akunena, ndipo ndinatenga kuchokera ku mutu umenewo, kuti ndikhale ngati ndakhala ndi phunziro la Sande sukulu mmawa uno; ndipo pamene ife tikukonzekera, ndi kukonzekera msonkhano wa usikuuno.

⁸ Ndipo Billy anati, “Muli bambo umo amene akudwala.” Anati, “Ine—ine—ine ndikanakonda inu mukanapitako ndi kukamuwona iye.” Chotero, ine ndinapita mchipindamo pompano. Ndipo m'bale wa pafupifupi usinkhu wanga, ndi mkazi wake, akhala mmenemo. Ndipo Mzimu Woyera unatsika pakati pathu mchipindamo pompano.

⁹ Tangoganizani, ndimangolankhula za msonkhano wa machiritso, ndipo pamenepo Iye anabwera. Mukuona? Ndipo Iye anamuuza m'bale uyu zonse zomwe iye anali atachita, ndi zomwe anakhala akuchita, ndi chimene chinayambitsa vuto lake, ndi komwe iye amachokera, ndi zonse za iye. Ndipo apo panali mthunzi waukulu wakuda umayandama mchipindamo. Kenako munayamba kuwala, kuwala, kuwala, ndi kuwala, zitatero Mzimu Woyera unatenga ulamuliro.

¹⁰ Tsopano, ine ndikuganiza bamboyo ali mu. . .penapake kumbuyo kuno tsopano. Iye ndi mkazi wake mwinamwake akulephera kulowa mchipinda muno, koma iwo amati akhalabe, mulimonse, pa msonkhanowu. Iwo abwera kuchokera kumtunda uko, pafupi ndi Yakima, Washington, ndipo ayendetsa. Ndipo iye ndi mtumiki wa Uthenga.

Koma kungowona chisomo cha—cha Mulungu pamenepo! Kumene, bamboyo anakhalapo kwa amisala ndipo amalandira zithandizo ndi chirichonse. Mzimu Woyera umawulula zonse izi. Pamene, madokotala amayesetsa zolimba kuti achite chirichonse chomwe iwo akanatha, mwinamwake, kwa bamboyo, koma izo zinangotengera kukhudza kwina kwakung'ono kuja kochokera kwa Mulungu, kuti kutembenuze fundelo. Mankhwala a manjenje ndi abwino, koma izo zimakhala ngati monga ife tingadzitchulire “kuwombera mu mdima,” inu mukudziwa. Inu, izo zikhoza kukupanga iwe kudwalika, mwaona, chifukwa izo

zimakupangitsa kuiwala chirichonse chimene iwe umachidziwa, nthawi imene iwo alowetsa mankhwala amenewo mwa iwe. Koma Ambuye Mulungu, mmene chisomo Chake ndi chifundo! Ndipo ngakhale ine ndisanapereke konse pemphero kwa iye, izo zinali zitatha kale. Mukuona? Izo zinangotengera chinachake icho cha Mulungu, kukhudza kwinakwake uko, kuti kuchite izo.

Ine sindikuyenera kuti ndinene izi. Eya. Ine ndayang'ananso, ndikumuwona bamboyo tsopano. Chabwino, ine sindimadziwa ngati mungakwanitse lero, kapena ayi.

¹¹ Ndinali kumusi uko kumene ine ndakhala ndikukhalako, sabata ino. Ine—ine—ine ndimawakonda abwenzi anga kumeneko. Ndi katchuthi kakang'ono misonkhano ikuluikulu iyi isanachitike, inu mukuona. Ndipo ine ndabwera kuno, kuti ndipite uko ndi kupita kukasaka agologolo ndi abale awa. Ndipo banja ili, mabanja, kani, omwe ine ndimakhala nawo uko, ndithudi ndi anthu achikondi. Ndipo bamboyo, m'bale weniweni, abwenzi; iwo ali.

Ndipo mmodzi wa iwo ndi wokonda a—agalu osakira kwambiri. Ndipo iye ali ndi khola lodzadza ndi iwo kumeneko. Ndipo—ndipo ine ndinawona galu wokongola wamng'ono kumeneko, kanthu kakang'ono, ndi kamene ine ndimakatcha kuti, “theka la usinkhu wa galu ndi utali wa agalu awiri,” inu mukudziwa, amene—amene amathamanga kuzungulira nyumba kumeneko. Ndipo ine ndinaganiza, “Mai, kodi Joe sangakonde atakhala ndi wina wonga ameneyo!”

¹² Ndipo, zoon, uko mu Arizona, sungathe kumugwiritsa ntchito iye. Iye angalowe mu akaloga, ndipo uko kungakhale kutha kwa iye. Kotero ndiye ine ndinati, nanenso, “Iwe sungakhale naye iye. Iwo sagwiritsa ntchito agalu kumeneko, ku dera ilo la dziko. Chifukwa, iwo, chabwino, iwo basi sangawagwiritse ntchito iwo. Iwo angati. . . nawonso, nyengo, a—momwe dzikolo lirili ndi akaloga, ndipo iwo akhoza kuphedwa.” Ndiyeno, zoon, galu kumeneko, a—nkhandwe, kapena chinachake chingamuphe iye, mwinamwake, mulimonse, ngati iye atati watuluka.

¹³ Koterono bambo uyu anati kwa ine, “Inu mukhoza kungomutenga iye.” Koma ine—ine sindikanamutenga iye. Ine—ine ndinayamikira zimenezo. Ndinadzapeza kuti, iye anali mmodzi wa agalu ake amene amawakonda.

¹⁴ Ndipo bambo uyu ali ndi mkazi wamng'ono wokonedwa ndi ana aang'ono. Ndipo tsiku lina, iye amayamba kubwerera mmbuyo ndi galimoto yake, ndipo iye anali ndi galimoto ya Oldsmobile iyi. Ndipo galu wamng'onoyo ndi wa pafupifupi kutalika *chonchi*, mwana wa galu basi. Ndipo iye anayendetsa molunjika nkumuponda iye. Oldsmobile ija inapita molunjika kwa galu wamng'onoyo, kumbuyo kwake *apa*, ndipo inamupelera iye pansu, kumene miyala mu kanjirako

inangofinyira mimba yake yaing'ono pansi apa, inu mukudziwa. Ndipo—ndipo mkazake wamng'onoyo, mmalo mothamangira naye galu wamng'onoyo ku vetenare... Zoona, a vetenare akanangomugonetsa iye nthawi yomweyo, ndi kumupha iye. Mukuona?

Apo panali mnyamata wina limodzi nane. Ndipo mwamsanga pamene iye anadzuka apo, anati, “Ngati uyo akanakhala galu wanga, ine ndikanamuwombera iye.” Anati, “Ndizo zonse. Kumusiya iye azivutika monga choncho?”

¹⁵ Ine ndinati, “Chabwino, tiyeni tisanuwombere iye.” Ine ndinati, “Tiyeni tidikire pang'ono chabe.”

Ndinamuchotsapo aliyense, ndipo ndinapita ndi kukamupempherera iye. Galu wamng'onoyo ananditsatira ine mpaka pakhonde. Ndipo iye, [Osonkhana akusangalala—Mkonzi.] inde, iye... Mukuona? “Zinthu zirizonse zimene inu muzikhumba, pamene inu mupemphera, mukhulupirire kuti inu mwalandira izo; inu mudzakhala nazo izo, zidzaperekedwa kwa inu.” “Zinthu zirizonse.” Ameneyo ndi Ambuye Mulungu wathu. Si choncho izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”] Iye—Iye ndi wopambana ndi wodabwitsa. Ndipo ife ndithudi tikumukonda Iye, mmawa uno; ndipo tikumuyembekezera Iye, ndi chidziwitso.

¹⁶ Ndinawona, tsiku lina, ba—banja lachikale, amayi ndi abambo a membala wabwino wa ili—gulu lino la okhulupirira. Ndipo amayiwo, oh, ine ndikuganiza iwo akuyandikira handiredi, ndipo bambowo ali, nawonso. Ndipo kwa pafupifupi zaka thwelofu bambo uyu anali asanayendepo; pa nsana wake, amangogona chafufu mimba. Kapena, amalephera kugonera cha m'mbali mwake, kapena chirichonse. Anagona pamenepo kwa zaka thwelofu. Ukalamba basi! Ndipo amayiwo tsopano ali pafupifupi usinkhu wa abambowo, ine ndikuganiza, penapake kuyandikira handiredi, ndipo kanthu kosauka kokalambako mutu wake sukugwira ntchito. Iye akuganiza winawake akutenga zonse zomwe iye ali nazo.

Ndipo ine ndinayang'ana pa... pozungulira tebulu, pa ife tonse, aang'ono ndi achikulire, titakhala pamenepo. Ndipo ine ndinati, “Kodi ife tikupita kuti? Kodi ife tikuchita chiyani?” Ndipo dona amene ine ndimakhala naye nthawi imeneyo, amenewo anali amayi ake ndi abambo. Ndipo ine ndinati, “Iwe ukupita komweko, nawenso. Ndendende, mmodzi aliyense wa ife.” Mukuona?

¹⁷ Tangoganizani za izo, mphindi chabe, ife tisanayambe phunziro lathu. Uko ndi kumene inu mwalunjika. Inu mukuvutikiranji? Kutu inu muthe kukhala moyo. Inu mukukhaliranji moyo? Kutu inu mudzathe kufa. Kodi izo sizingakhale zopusa kwambiri ngati ife sitingavomereze thandizo la Mulungu la Moyo Wamuyaya? Kodi ife tingaganizire

chiyani? Ndi chiyani—pangakhale chiyani pa mtima pathu, chimene chingakope chidwi chathu kutichotsa...kwa chirichonse? Bwanji ngati inu mutakhala ndi madola handiredi milioni, ndipo inu nkukhala mwini wa mzinda wa—wa Indiana, kapena mzinda wina uliwonse, kapena ngakhale fukoli, kapena, ngakhale izo zitakhudza, dziko lonse?

Inu mukadzakhala moyo nthawi yaitali, inu mudzayenera kuti mudzafike kwa chimenecho, nanunso. Mukuona? Ndipo pang'onopang'ono, tsiku ndi tsiku, nthawi iliyonse imene mtima wanu ugunda, inu mukupita molunjika kwa chimenecho. Mukuona? Inu, sikuti mwapambana. Inu muli kumbali yogonja, ndipo, inu, inu mudzayenera kuti mudzagonje. Koma kumbukirani lonjezo, lakuti, "Iye amene adzataya moyo wake chifukwa cha Ine adzaupeza iwo." Tsopano, ndi chiyani chimene chingakhale chuma chopambana kuchipeza kuposa Moyo, ngakhale inu mutapeza dziko lonse kuti likhale lanu? Koma, ngati inu—ngati inu mudzapeza Moyo, inu mudzapeza chinthu chachikulu kwambiri chimene chingapezedwe. Ine ndikufuna kuti . . .

¹⁸ Ndinayang'ana kumanzere kwanga ndipo ndawonanso, pompano, chikho china cha chisomo cha Ambuye. Pafupifupi masabata pang'ono apitawo, ine ndinaitanidwa pa foni. Ndipo membala wokondedwa wa tchalitchi chino, kapena thupi ili . . .ine sindikufuna kutchula izi mochulukwa kwambiri ngati tchalitchi. Ine—ine ndikufuna kutchula ichi, kuti . . .

Monga ine ndimayankhula ndi anthu ena, iwo anati, "Chabwino, kodi ndinu wa tchalitchi chiti?"

Ine ndinati, "Ine ndiribe . . ."

"Ndinu wa chipembedzo chiti?"

Ine ndinati, "Palibe."

Anati, "Chabwino, ndinu wa chiyani?"

Ine ndinati, "Ufumu."

¹⁹ Ufumu! "Ndipo ndi Mzimu umodzi ife timabatizidwira mu Ufumu umenewo." Mwa Mzimu umodzi, tonse, timalowa mu Ufumu uwu! Yesu anati, "Muzipemphera, 'Ufumu Wanu udze. Kufuna Kwanu kuchitidwe pa dziko, monga ziliri Kumwamba.'" Tsopano, Iye anaima tsiku lina pa Phiri la Chiwalitsiro, Iye anati, "Indetu Ine ndinena ndi inu, kuti ena aima pano, sadzalawa imfa, kufikira iwo adzawone Ufumu ukubwera mu mphamvu." Izo zinawonetsedweratu, monga ife takhala tikudutsa zimenezo, Phiri la Chiwalitsiro. Ndipo Baibulo linati, "Ufumu wa Mulungu uli mkati mwanu." Koteru, awa ndi anthu a mu Ufumu amene amadzinenera kuti kuno si kwawo. Kuno si kwathu. Ife tikuyembekezera Kubwera kwa Mfumu, kudzakhadzikitsa Ufumu.

²⁰ Ine ndinaitanidwa mwadzidzidzi, ndi—ndi m'bale wokalamba amene wakhala ngati bambo kwa ine. Ndipo iye. . . Ine sindinadziwane naye iye pakale, koma ine ndikukumbukira tsiku limene ine ndinamutengera iye muno ku ubatizo wa mmadzi. Ndipo bamboyu pompano akhala usinkhu wa zaka nainte-wani. Ndipo mkazi wake wokonedwa anandiimbira ine, ndipo iye pokhala namwino, anati, "Iye anali ndi kulephera kwathunthu kwa mtima." Pambali pa zimenezo, iye anali. . . O, ine nditchula. . . ndikulephera kutchula dzinalo. Matenda a mtima. [Mlongo akuti, "Mtsempha."—Mkonzi.] Matenda a mtima a mtsempha. Zikomo inu. Matenda a mtima a mtsempha, ndi kulephera kwathunthu kwa mtima. Adokotala sanapereke chiyembekezo chirichonse, nkomwe. Ndipo bamboyu anali akufa, ndipo iye anandiitanitsa ine.

²¹ Ndipo ine ndinakwera Ford yanga yakale yaing'ono, ndipo ndinauyamba ulendo wopita ku Ohio, mwamphamvu mmene ine ndikanathera. Ndipo sindimadziwa, limodzi la gudumu langa linali litachoka mu mzere, zinapangitsa tayala kusendeka. Ndipo koteru ndiye ine. . . nditafika kumeneko. Ndikutuluka pothirira mafuta, pafupifupi leveni koloko. Ine ndinali kudandaula za iye. Ine—Ine ndimamukonda iye. Ndipo ine ndikudziwa, ngati—ngati izo ziti zipitirirebe, Ambuye akachedwa, bwanji, pompano kapena mochedwerapo, ife tiyenera kuti tidzasiyana wina ndi mzake.

²² Koma, izo sizidzalepheretsa Mkwatulo, tsopano. Mukuona? Ayi. Iwo adzayambirira kubwera, ndiye. Iwo anachita mwayi, amene anatsogola. Iwo adzayambirira kubwera. Mukuona? Mukuona? "Ife amene tiri moyofe ndipo tatsalira, pa Kudza kwa Ambuye, sitidzawatchinga kapena kuwalepheretsa iwo amene akugona. Lipenga la Mulungu lidzawomba; akufa mwa Khristu adzauka poyamba. Ndiye pamene maso athu adzawone okonedwa athu, pamenepo ife tidzasinthidwa, mkamphindi, mu kuthwanima kwa diso, ndipo limodzi ndi iwo tidzakwatulidwa pamodzi." Mukuona? Iwo amene anatsogola anachita mwayi kuposa iwo amene ali moyo.

²³ Pamene ine ndimachoka pothirira mafuta, basi itangokwana leveni koloko, Mzimu Woyera unanena kwa ine, "Usadandaule za iye. Iwe udzamugwira dzanja lake, pa msewu kamodzinsu, ndipo iye adzabwera ku tchalitchi," bambo wa usinkhu wa zaka nainte-wani, akufa.

Pamene ine ndinakumana ndi mkazi wake ndi okonedwa ake mu chipatala ku Lima, iwo anandiuza ine za mmene aliri. Ndinalowamo, ndinayang'ana pa iye m'menemo. Iye anati, "Koma iye ndi winawake wachilendo." Anati, "Iye—iye anayamba kusintha kukhala bwino, pa leveni koloko." Chabwino, ndipo ine ndinali. . . Ambuye anali atawawonetsetsa anthu amenewo zinthu zambiri, iwo amadziwa kuti ine sindinangonena zimenezo. Chifukwa, iwo ananena kwa ine

poyambirira, “Iye anayamba kusintha.” Iwo amadziwa kuti ine ndiwauza iwo zoono.

²⁴ Koteru, Lamlungu lapitali, pamene ine ndimapita ku Blue Boar Cafeteria mu Louisville, kumene ine ndikuganiza pafupifupi eyite peresenti ya gulu lino mumasonkhanako Lamlungu masana, kukadya, kodi ine ndinamuwona ndani akubwera chotsika mu msewu? Ine ndikukuuzani inu, mtima wanga unanjenjemera pamene ine ndinamuwona M’bale wathu Dauch akubwera mu msewu, ndendende zimene Iye anandiuza ine. Ine ndinagwira dzanja lake, pa—pa msewu.

²⁵ Kenako ine—ine ndinabwerera kuno kwa usiku wa Lamlungu lapitali ndipo ndinadzayankhula pa phunziro la umodzi, la *Kulumikizana Kwa Chizindikiro Cha Nthawi*. Koteru . . . Ndiyeno izo zinapangitsa izo kukwaniritsidwa, basi chimene Iye ananena. Ndipo apa iye wakhala mu tchalitchi lero, pomwe pano pafupi ndi ife, ngati chikho cha chisomo cha Mulungu. Pamene ndinali kugwira dzanja lake pansi pa hema, hema wa okisejini amene iye analimo, ine ndinati, “M’bale Dauch, inu mukhala bwino. Ine ndidzakuwonaninso ku tchalitchi. Izo, ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE.” Mukuona? Ndi uyu wakhala apayu mu tchalitchi, pomwe pano tsopano, M’bale Dauch.

²⁶ Ngati ine sindikulakwitsa, mtumiki amene ine ndimamukamba, mphindi pang’ono zapitazo, Mzimu Woyera unadzabwera ndi kudzaulula zinthu zonse izi; unamuza iye mmene izo zinachitikira, ndi kumuza iye zimene anachita; mmene zinachitikira, m’mene zinadzakwaniritsidwira, zonse zomwe zakhala zikuchitika kuyambira nthawi imeneyo, ngakhale kufika ku khalidwe la banja lake, ndi zonse zokhudza izo. Ndipo ndinamuza iye, kuti, “Izo zatha.” Ndipo mtumikiyo wakhala pomwe pano, kudzanja lamanja. Mungangokweza dzanja lanu m’mwamba, bwana? Pamenepo, iye ndi mkazi wake, ndendende, pompano.

Apa pakhala M’bale Dauch, pomwe pano tsopano. Oh, mai!

²⁷ Kodi Iye si wodabwitsa? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] “Zinthu izo zimene zinali, zimene ziripo, ndipo zidzakwaniritsidwa.” Mboni imodzi, ziwiri, zitatu. “Zinthu zomwe zinalipo, zomwe inu mwachita; zinthu zimene zikuchitika tsopano; ndi zinthu zomwe ziti zidzachitike.” Ndipo nthawi iliyonse, ndendende, ndendende pa Mawu. Uyo ndi Mulungu yekha yemwe angachite zimenezo. Oh! Kodi sindife okondwa kwambiri chifukwa cha zinthu izi? [“Ameni.”]

²⁸ Tsopano, chifukwa chimene ine ndimatenga ka nthawi pang’ono kowonjezera, Billy amayenera kuti apite akamtenge mkazi wake ndi mwana. Ndipo iye anati, “Adadi, musakayambe kulalikirira mpaka ine nditabwerera.” Koteru, ine—ine ndikuganiza iye wabwera tsopano. Ndipo ine ndikuyenera

kukhala ndi nthawi yokwanira imeneyo, mulimonse. Ndipo ine ndikuyesera kuti ndichoke ku ma ora foro otopetsa awa amene ine ndimakuikanimu inu nonse pano, ndi kuzipanga izo maminiti sate-faifi, forte, inu mukuona, ndi kuyesera kusunga izo.

²⁹ Tsopano, ine ndinayamikiridwa nthawi ina mu Chicago. Ine ndinazifikitsa izo maminiti sate, kapena chinachake, maminiti sate-faifi. Ndipo Lamlungu lapitali usiku anali maminiti forte-faifi okha. Billy anati, “Inu mukusantha kwenikweni, adadi. Ine ndikukunyadirani inu, chifukwa cha izo.”

³⁰ Chabwino, mwinamwake, m'mawa uno, kuti tizipange izo mwa mtundu wa Sande sukulu, ine sindikusungani inu nthawi yaitali. Kenako inu mutha kutuluka ndi kukakhala ndi nkhomaliro yanu, ndi kukapempherera, ndi kubwerera usikuuno pa msonkhano wa machiritso. Ife tipanga mzere wa pemphero usikuuno ndi kupempherera odwala.

³¹ Tsopano, ngati inu mukudziwa anthu aliwonse pozungulira, kulikonse, amene akudwala ndipo akufuna kuti adzapemphereredwe, inu muwabweretse iwo kuno usikuuno. Mukuona? Ngati inu mukusowa kuti muwabweretse iwo, mulimonse, mudzawabweretse iwo kuno. Mukuona? Ndicho chinthu chenichenicho, ndicho, kuwabweretsa iwo kuno usikuuno. Ife tonse timakumana pamodzi. Mwanjira imeneyo...Ndizovuta kuitanizana, kupita malo ndi malo; zotozozo umamusiya wina, ndipo amakhala ndi kumverera moipa. Koma ngati ine nditangoti ndawabweretsa iwo onse pamalo amodzi, ndiye ine ndikhoza kudzapempherera iwo. Tsopano, ngati inu munga...Ngati anthu akufuna kuti apemphereredwe, iwo...Inu mukuti, “Iwo angatero?” Oh, ndithudi. Iwo adzapemphereredwa. Mudzawabweretse iwo. Ambuye akalola, ife tidzakhala tiri pano, kudzapempherera aliyense. Chifukwa, ine ndikumverera kuti chikoka chachitatu chija chikuyamba kusantha, inu mukuona, ndi—mkati mwa ine. Ndipo ine—ine—ine ndikufuna kumupempherera aliyense.

³² Tsopano tiyeni titsegule, m'mawa uno ku Lemba lozowowereka lakale pamene ine ndinatenga mwaliwiro usiku wathawu, pokhala watulo kwambiri, ndipo ndinalemba Malemba angapo kuti apite ndi ilo. Ndikutenga ngati mothandizira. Ine ndinamva m'bale wina, kamodzi, akugwiritsa ntchito phunziro ili. Ndipo ine ndinaganiza...Ine ndinalemba izo. Ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndikukhulupirira ine ndizilemba izo, chifukwa izo zingadzakhale zothandiza.”

Nthawi zambiri ife timachita zimenezo. Ine ndawona, ambiri a inu pano, munali ndi chidutswa cha pepala. Ndipo mtumiki akhoza kumanena chinachake, ndipo ndiye inu—inu mukhoza kugunda nsonga imeneyo, chinachake chikhoza kugunda mkati mwanu. Ndiyeno ngati Mzimu Woyera ukuchita zimenezo, ndiye

iwe umayamba kumanga kuchokera pa nsonga yomweyo iyo pomwepo, uthenga wa Ambuye. Ndipo izo ndi zabwino. Ine ndawonapo mmisonkhano, kulikonse kumene iwe upita, basi kumangokhala alaliki ndi anthu akulemba. Izo ndi zabwino. Ife—ife tiri pano, ndicho chimene ife tadzera pano, ndi kuti tidzayesere kuthandizana wina ndi mzake pa njira izi.

³³ Ndipo tsopano tiyeni titembenezire ku Chivumbulutso, mutu wa 3, ku mibadwo ya mpingo, kubwereza m'badwo wa mpingo. Koma tsopano ife tiri...ife...pamenepo. Eya. Ine ndikhoza kutenga mutu umodzi uwu, ndipo ndi Mzimu Woyera, nkulalikira pa Iwo zaka handiredi ndipo osakhoza konse kutulutsa chimene chiri mwa Iwo. Chifukwa, mu mutu umodzi uwu, monga mitu ina yonse ya Baibulo, Izo zonse zikumangirizana pamodzi.

Ndipo ndikufuna kutenga phunziro langa, m'mawa uno, la izi: *Kodi Ndingagonjetse Bwanji?* Tsopano, ine ndinasankha ili chifukwa ine ndikuganiza kuti ino ndi nthawi imene ife sitikuyenera kulola Mzimu wa chitsitsimutso kuti ufe. Ife tikuyenera kukhala mu chitsitsimutso, otsitsimutsidwa pafupipafupi, tsiku ndi tsiku. Paulo anati iye amayenera kuti “adzifa tsiku ndi tsiku, kuti Khristu azikhala moyo.” Ndipo ife tisamalole kuti chitsitsimutso chimenecho chidzifa, mwa ife.

Tsopano, Chivumbulutso, mutu wa 3, ndipo kuyambira ndi ndime ya 21, ife tikuwerenga izi.

Kwa iye amene agonjetsa ine ndidzamalola kuti adzakhale ndi ine mu mpando wanga, ngakhale monga ine... ndinagonjetsa, ndipo ine ndakhala pansu ndi Atate anga mu mpando wake.

Iye amene ali nalo khutu, msiyeni iye amve chomwe Mzimu ukunena kwa mpingo.

³⁴ Kodi inu munazindikira do—dongosolo la zimenezo? Mukuona? “Adzakhala ndi Ine mu mpando Wanga,” osati “pa mpando Wanga.” “Mu Mpando Wanga,” izo ndi mu ulamuliro Wake. Mukuona? Ndipo apo, monga—monga Khristu ndiye Wolamulira, Wolamulira wa pa mpando pa nthawi iyi, wa ulamuliro wathunthu wa Mulungu, chomwechonso Mpingo udzakhala ndi Iye, Mkwatibwi adzakhala ndi Iye, mu mpando Wake, mu ulamuliro wonsewo. Mukuona? Osati “pa mpando Wanga,” koma “mu mpando Wanga,” mwaona, kumene ulamuliro Wake ukufikirako. Mpando umakhala mu ulamuliro, ndipo—ndipo ulamuliro umangofikira kutali monga mmene malire ake akuchitira. Ndipo izi ndi kuchokera ku Muyaya mpaka ku Muyaya. Tangoganizani za izo!

³⁵ Tsopano, pamene ife tikuphunzira izi, cholinga changa cha izi si kungobwera kuno kudza—kudzayanjana ndi anthu inu. Chimene, ine ndimakonda kuchita zimenezo. Koma ngati—ngati ine ndikanakhala ndi mwayi wochita zimenezo, ine

ndikanabwera kunyumba kwanu, ndi kudzakugwirani chanza ndi kudzayankhula nanu, ndi kudzakhala pansi, kudzadya nanu chakudya cha madzulo; ndi kukhala pansi, pansi pa mthunzi wa mtengo, ndi kuyankhula ndi kucheza pang'ono.

Koma pamene ife tibwera kuno, ife timabwera kuno kwa cholinga chimodzi chenicheni. Ino ndi nyumba yokonza. Uwu ndi mpando wachifumu. Uwu ndi mpando wachifumu wa Mulungu, ndipo chiweruzo chimayambira mnyumba ya Mulungu. Ndipo pano ndi pamene ife timabwera pamodzi, kudzasonkhana mu chikondi, wina ndi mzake, pakuti ndi Akhristu okha amene amatha kukonda. Koma, pano, ife tima—ife timakhala pansi pa—pa—pa—pa utsogoleri wa Mzimu Woyera. Mzimu Woyera uli pakati pathu. Ndipo ife tiri pano kuti tidza. . . kudzadzifufuza pakati pathu, kuti tidzawone pamene malo athu operewera ali, zofooka zathu, ndi mmene ife tingafikire pomwe ife tikuyenera kukhala, kufika kumene ife tikuyenera kukhala tsopano; pomwe ife tiri, ndi pamene ife tikuyenera kukhalapo. Ndipo ndizo zomwe ife tikuphunzira. Atumiki amaphunzira malo amenewo, chifukwa cha anthu awo. Pamene iwo awawona anthu, chosowacho, ndiye iwo amayambira pa chimenecho.

³⁶ Tsopano, posakhalitsapa, ine ndikuganiza kuti mpingo mwinamwake udzikhala ukutenga mphondero yaing'ono yokwerera mmwamba pa nthawi ino. Ine sindikukonza zochita izo m'mawa uno, za kuwonetsera zinthu izi. Koma ine—ine ndikuganiza, posachedwapa, Ambuye akalola, ife tisanalalikire pa Malipenga awo, ine ndikufuna kuti—kuti—kuti ndidzabweretse kwa Mpingo chinachake chimene—chimene inu mukuyenera kuchidziwa, ine ndikukhulupirira, tsopano.

³⁷ Ndipo tsopano ife tikuyankhula pa izi, “kugonjetsa.” Mawu akuti *kugonjetsa*, ndithudi, inu mukudziwa chimene iwo amatanthauza. Iwe umayenera kukhala ndi chinachake choti uchigonjetse. Ndipo m'badwo wa mpingo uno umene Mzimu Woyera umawukamba apa, ku M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya, monga ife tangodutsa kumene iwo, umafunika chidzudzulo. Laodikaya amayenera kudzudzulidwa, chifukwa cha kwake—kutsutsa kwake pa Khristu. Iwo unali utamuika Khristu panja, mu—mu m'badwo wawo. Ndipo Khristu anali panja, akuyesera kuti abwererense mkati. Chimenecho ndi chikondi. Iye atatha kuikidwa panja pa nyumba Yake Yomwe, anali akuyesera kuti abwerere mkati, ndipo anati, “Iye amene ati adzatsegule khomo, Ine ndidzabwera mkati kwa iye.” Mukuona? Mpingo, pawokha, mwathunthu, unali utamuika Iye panja.

³⁸ Koma tsopano zindikirani. Kuitana Kwake apa si kwa mpingo wokha. “Iye amene agonjetsa.” Mukuona? Osati mpingo; iwo ukanakhala mkazi, mwaona, thupi la mpingo. Koma izo ndi “iye amene agonjetsa,” munthu payekha amene ati agonjetse, tsopano.

³⁹ Ndipo Laodikaya anali nazo izo zikubwera kwa iye. Tsopano ife tikuwona, ndiye, podziwa kuti uno ndi M’badwo wa Laodikaya, ndiponso podziwa kuti m’badwo uno ukusowejera chidzudzulo chakuthwa kuchokera kwa Mulungu. Iwo ukusowejera chidzudzulo chakuthwa. Ndipo pamene azibusa athu akhala ofewa kwambiri ndi olekelera, monga agogo aamuna ena okalamba kwa zidzukululu zawo, chirichonse chimene iwo amachita chimakhala chabwino. Ndipo iwo ali . . .

⁴⁰ Izo zanenedwapo mochuluka, kuti Mulungu ndi Mulungu wabwino, mpaka iwo amayesera kuti amupange Mulungu kukhala agogo aakulu olekelera. Inu mukuona? Koma Iye siali. Iye ndi Atate, ndipo Atate achirungamo, okonza. Ndipo chikondi nthawizonse chimakonza. Mukuona? Chikondi chimakonza. Ziribe kanthu kaya zipweteka bwanji, icho chimakonza.

Mayi weniweni amawakonza ana ake. Bambo weniweni amawakonza. Mukuona? Ngati iwe ungokhala wofewa ndi wolekelera, ndi kumazilolera izo . . .

⁴¹ Ine ndinali kuwoloka pa chipika chakale tsiku lina, ndikutsikira—tsidya lina, kapena chimene chimatchedwa chidzenje. Ndipo ine ndinalumphira pa chipika ichi. Kunja kwake, icho chimawoneka chabwino, chimawoneka ngati chipika chachikulu chakale cha mthundu. Koma pamene ine ndinalumphira pa icho, oh, gawo lalikulu la icho linanyotsokapo. Icho chinali chitavunda kwenikweni ndipo chitafewa. Ine ndinati, “Umo ndi m’mene akukhalira Akhristu.” Iwo afa mu tchimo ndi nkulakwitsa, nthawi yaitali, mpaka asanduka olekelera. Iwo sakumakhala ndi kulemelera kulikonse, nkomwe. Iwo—iwo sakudziwa kuti kugonjetsa kumatanthauza chiyani. Ndipo ine ndinayamba kuganizira za mutu uwu, nthawi imeneyo. Kugonjetsa, kusunga Moyo mwa iwe. Pamene moyo unachokamo, ndicho chimene chinachifikitsa chipikacho ku chikhaliidwe chimenecho. Mukuona? Ndipo izo zinapangitsa icho kuipa kuposa kale pamene icho chinali pa nthambi komwe kunali madzi.

⁴² Ndiyeno, apo, inu mukamtenga Mkhristu, amene ayenera kukhala Mkhristu, akalola Moyo wa Mulungu kuti uchoke mwa iye, ndi chomuchitikira, chimwemwe chotumikira Khristu; ndi, kumakhala mu tchalitchi chimene zimenezo zikuchitika, iye amavunda mwachangu pawiri, kulondola, amakhala motsikirapo.

⁴³ Kotero, ngati ife tikuyesera kuti titsatire Uthenga wa ora, kapena mwinamwake gawo ili la Uthenga, ife tiyenera tidzikhala nthawizonse mu Moyo wa Khristu. Mukuona? Chifukwa, ngati izo sizitero, iwe ungokhala, ndi kumadziwa Izo, zinthu izi zimene iwe uyenera kuti uzizichita, ndipo osazichita izo. Baibulo linati, “Iye amene adziwa kuchita bwino, ndipo nkusachita izo, kwa iye ndi tchimo.” Ndiye iwe umadzakhala

wolekelera, wovunda, pamene iwe walekanitsidwa kwa Moyo wa Mulungu. Koteru, limbikirani ndi zonse zomwe ziri mwa inu, kuti mudzikhala mu Moyo wa Khristu, kuti inu mukhale obala zipatso.

⁴⁴ Ife tikuwona m’badwo uno umene ife tiri nkukhalamo. Iwo ndi umodzi wa mibadwo yopambana kwambiri ya mibadwo yonse. M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya uwu ndi wopambana kwambiri mwa mibadwo ya mpingo yonse, chifukwa iwo ndi kutha kwa nthawi ndi kulumikizana kwa Muyaya. Ndipo, ndiye, ndi m’badwo waukulu wochimwa kwambiri. Muli tchimo lochuluka mu m’badwo uno kuposa umene unayamba wakhlapo. Ndipo mphamvu za Satana ziri—nthawi zambiri zikumakhala zovuta kulimbana nazo kuposa mmene izo zinaliri mu m’badwo uliwonse. Mukuona? Pano!

⁴⁵ Kumbuyo uko mu zaka zoyambirira, m’Khristu amatha, pa kudzinenera kwake kokhala mpingo... kukhala wa Khristu, amakhoza kudulidwa mutu chifukwa cha izo. Iye amatha kuphedwa, ndi kuchotsedwa mu umphawi wake, ndi kupita kukakumana ndi Mulungu, mwamsanga.

Koma tsopano mdani walowamo, mu dzina la mpingo, ndipo izo ndi zonyenga kwambiri. Uno ndi m’badwo waukulu wa chinyengo. Nthawi imene, Khristu anati, “Mizimu iwiriyo idzakhala yoyandikana kwambiri mmasiku otsiriza mpaka iyo ikanadzanyenga Osankhidwa kumene ngati kukanakhala kotheka.” Mukuona? Mukuona? Mukuona? Kumbukirani, Khristu analankhula za anthu osankhidwa a tsiku lotsiriza. Mukuona? “Iyo ikanadzanyenga Osankhidwa kumene ngati kukanakhala kotheka.” Moyandikana kwambiri! Anthu amakhala, anthu akhoza kukhala mwachiyero, moyo woyera; osakhala ochimwa, achigololo, ndi oledzera, ndi amabodza, a njuga. Iwo akhoza kukhala pamwamba pa izo, ndipo nkusakhala nawobe Iwo.

⁴⁶ Uno ndi—m’badwo wa Moyo, Moyo wa Khristu mwini, pamene, zi—zipangizo za Thupi Lake, zimene zinali mwa Iye.

Choyamba, pansu pa kulungamitsidwa, ubatizo wa m’madzi. Chachiwiri, pansu pa Kubadwa kwatsopano, kwa Wesley, kuyeretsedwa, chimene chimayeretsa. Ndipo chachitatu, pansu pa ubatizo wa Mzimu Woyera, kukachiika chida choyeretsedwacho mu utumiki. Mukuona? Mawu akuti *kuyeretsa* amatanthauza, ndi mawu Achigiriki apawiri amene amatanthauza “kuyeretsedwa ndi kuikidwa pambali ku utumiki,” kuikidwa pambali ku utumiki. Tsopano Mzimu Woyera umachiika icho mu utumiki. Mukuona?

⁴⁷ Ndipo ife tikuzindikira, “Pamene mzimu woyipa uchoka pa munthu, iwo umakayenda mmalo owuma.” Izo ndi ndendende zomwe mpingo wachita, Abaptisti, Amethodisti, iwo amene amakhulupirira mu kuyeretsedwa. “Ndiye,” Yesu anati, “mzimu

woyipa umene unatulukawo, umabwereranso ku thupi la mpingo ili ndi kudzaizepa nyumbayo itakonzedwa, itasesedwa moyera, kumakhala woyera, miyoyo yoyera.” Zonse zabwino. “Koma kenako ngati nyumbayo siidzadzidwa, siilowedwa, ndiye iye amadzalowamo ndi ziwanda zina seveni woipa kuposa mmene iye analiri, ndipo gawo lomaliza la malo awa ndi kaseveni kuipa kwake kuposa mmene zinaliri pa nthawi yoyamba.” Iwo zikanakhala bwino akanangokhala Achilutera, kuposa mmene zikanakhallira kuti alandire Kuwala kumeneko ndi kulephera kuti akutsatire Iko. Chomwechonso ndi Achipentekoste, mwaona, inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, nyumbayo yakonzedwa.

⁴⁸ Pamene ine ndinali kuyankhula ndi winawake, tsiku lina, ndinati, “Iwo amakhala osamalitsa kwambiri, ngakhale ambiri a magulu a achiyero, samatchula kuti Holy Ghost, ‘Holy Ghost,’ chifukwa iwo adzizindikiritsa okha ndi Achipentekoste pamene iwo achita zimenezo. Iwo amati, ‘Holy Spirit,’ mwaona, kuwopa kunena kuti, ‘Holy Ghost.’” Chifukwa, Achipentekoste, anthu wamba, amangowutcha Iwo chimene Baibulo limanena, “Holy Ghost.” Chimene, Holy Spirit ndi Holy Ghost ndi chinthu chomwechomwecho. Koma iwo amakhala osamalitsa kwambiri za izo. Iwo samafuna kuti adzindikiritsidwe ndi anthu oyankhula mmalirime awo; ndipo umenewo ndi Mzimu Woyera, Pawokha. Mukuona?

Chimachitika ndi chiyani zikatero? Pamene m’dani, amene anatuluka pansu pa kuyeretsedwa, amene anachapidwa, akabwerera ndi kudzapeza nyumbayo kuti siinadzadzidwe ndi Mzimu Woyera, tsopano boma la mpingo lalumikizana ndi—ndi gulu la mipingo, ndi Mgwirizano wa Mipingo ya Mdziko. Ndipo ndi boma tsopano limene likuwulumikizitsa iwo ndi chi Roma Katolika ndi zonse za izo, ndipo tsopano izo ndi zoipa ka seveni kuposa mmene zinaliri pamene iwo unkatuluka mu Chilutera. Apo ndi pamene munthu wawutengera iwo.

⁴⁹ Ndiyeno tawuwonani M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya utatha kulandira Mzimu Woyera, ndi chidziwitso ndi Mzimu wa Mulungu mkati mwa Iwo, ndiyeno ntchito za Mulungu nkumakanidwa ndi iwo, ndi kumadzitcha Izo “ntchito zoipa.” Ndiye nanga bwanji zimenezo? Apo ndi pamene Khristu akuikidwa kunja kwa mpingo Wake Womwe. Mukuona? Iye. . . Izo sizinamuwonetse Iye ali mu mpingo mpaka izo zitafika ku Laodikaya; ndipo pamene Iye anafika ku Laodikaya, Iye anali ataikidwa kunja kwa mpingo Wake, akuyesera kuti alowenso mkati.

⁵⁰ Tsopano, taonani, kulungamitsidwa sikunamuike Iye mkati. Kuyeretsedwa kunangomuyeretsera Iye malowo. Koma pamene ubatizo wa Mzimu Woyera unabwera, iwo unadzamuika Iye mwa anthu. Ndipo tsopano iwo anamukana Iye, pamene Iye anayamba kudziwonetsera Yekha, kuti Iye ali yemweyo

dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iwo anamukana Iye chifukwa iwo achita chipembedzo, ndipo mzi—Mzimu wa Ambuye sukugwirizana ndi chipembedzo chawo. Inu mukumvetsa tsopano? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Izo, iwo anamuika Iye panja. “Ife sitikufuna kukhala ndi chochita chirichonse ndi zowerenga maganizo izi. Izo ndi—izo ndi za mdierekezi. Izo ndi m’bwebwe. Kapena . . .” Mukuona?

Iwo sakumvetsa. “Maso, ndipo osatha kuwona; makutu, ndipo osatha kumva.” Mukuona? Mulungu amangotsegula maso mmene Iye akufunira. “Iye amamuumitsa amene Iye wamuumitsa, Iye amakhumba kutero, ndipo—ndipo—ndipo amapereka Moyo kwa iwo amene Iye wakhumba kuwapatsa.” Icho ndi chimene Lemba linanena.

⁵¹ Tsopano, ife tikuwona maora awa amene ife tirimo, siteji ino, ndipo ife tikuwona chimene izo zinali. Ndipo Mzimu Woyera ukudzudzula m’badwo umene unamutulutsa Iye panja. Koma, mu zonsezo, kodi inu munazindikira, “Kwa iye amene agonjetsa?” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ngakhale mu m’badwo wa mpingo, wachidziko woyipa uja, “Iye amene agonjetsa.”

⁵² Ife tikupeza apa kuti Mulungu nthawizonse wakhala ali nawo agonjetsi. Iye wakhala ali nawo agonjetsi mu m’badwo uliwonse. Pakhala pali nthawizonse, nthawi iliyonse, mu m’badwo uliwonse umene wakhlapo pa dziko lapansi, Mulungu nthawizonse wakhala ali ndi winawake amene Iye amaikapo manja Ake, ngati mboni pa dziko lapansi. Iye sanayambe wakhlapo wopanda mboni, ngakhale nthawizina m’modzi yekha. Koma winawake amagonjetsa, tsopano, monga oyera akale.

⁵³ Ndipo mu—munthu wabwino kwambiri, wophunzira, anali kunena, nditatsiriza *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri*, iye anati, “M’bale Branham, inu pokhala wo—wotaipa, wofanizitsa, kani,” anati, “ndi motani mu dzikoli muti mudzawuike Mpingo umenewo mu Mkwatulo popanda kudutsa nthawi ya Chisautso, moimira?” Iye anati . . .

Inu mukuona, ngati icho chiri choimira, apo payenera kukhala . . . apo payenera . . . Ngati pali choimiridwa, pakuyenera kukhala choimira komwe choimiridwacho chikuchokerako. Ndipo chirichonse chimene ine ndikunena, chimene chiri choona, chiri nacho choimira. Icho chiri nacho choimira. Inu muli ndi mthunzi. Ndipo Baibulo linati, “Zinthu zakale zinali mthunzi wa zinthu zatsopano ziri nkudza.”

Iye anati, “Koma tsopano inu mwatenga Chipangano Chakale ngati mthunzi. Tsopano,” iye anati, “inu muchita nawo chiyani Mpingo uwu?”

⁵⁴ Munthu uyu amachokera ku . . . Munthu wotchuka, mphunzitsi wotchuka amene ali bwenzi wapamtima wanga,

munthu wabwino kwambiri, ndipo iye ndi m'bale wachikondi. Ine—ine sindingayerekeze kunena mawu amodzi omutsutsa m'baleyo. Ine sindingatero, mulimonse. Ngati—ngati a . . . Ngati Mkhristu, ine sindinganene kalikonse komutsutsa iye. Iye—iye—iye sagwirizana nane ine pa phunziro limodzi ilo, koma iye—iye ndi m'bale wanga wofunika. Iye timadya limodzi. Ndipo, oh, iye ndi munthu wokoma basi. Ine ndimatenga magazini ake, ndimawerenga zolembe zake. Ndipo iye amalemba zina za ine, ndi zina zotero. Ndipo ine ndatengapo mitu yambiri kuchokera pa zimene ine—ine ndawerenga—ndawerenga za zolembe zake, ndamumvapo iye akunena. Iye ndi munthu wachikulire, koma iye—iye sagwirizana nane basi. Ine ndimayamikira zimenezo, za kuwona mtima kwake. Ngakhale iye samatero basi, ena ongokankhidwa awa, samangogwirizana ndi zirizonse zimene iwe ukunena. Iye amakhala ndi kumvetsa kwake kwake, ndipo iye amaima ndi zimenezo. Ine ndikuyamikira zimenezo. Ndipo iye ndi munthu wabwino. Oh, ine—ine sindine mphunzitsi kapena wophunzira, nkomwe, koma munthu uyu ali zonse ziwiri mphunzitsi ndi wophunzira.

⁵⁵ Koma ine—ine sindingagwirizane naye iye, chifukwa ine sindimaziwona izo. Koma, izo sizikukhudzana ndi chipulumutso, izo ndi zokhudzana ndi Kubwera kwa Ambuye. Iye amawona kuti Mpingo uyenera kudutsa nyengo ya Chisautso, kuti udzayeretsedwe. Ine ndimati Magazi a Yesu Khristu anawuyeretsa Mpingo. Mukuona? Iwo sukusowa . . .

Ine ndimakhulupirira kuti mpingo udzadutsa nyengo ya Chisautso, bungwe la mpingo, koma Mkwatibwi sadzatero. Kodi iwe ungasankhe mkazi amene iwe uyenera kumuyeretsa usanamukwatire? Mukuona? Mkwatibwi wa Khristu ndi wopatulidwa, ndipo Iye ndi Wosankhidwa. Ndipo Iye ndi Mkwatibwi wa Mulungu, Mkwatibwi wa Yesu Khristu.

⁵⁶ Ndipo tsopano iye anati, “Kodi inu muzifanizitsa motani izo, ngati Mkwatibwi ameneyo adzapita, adzapita Iye asanadutse nthawi ya Chisautso?” Ndinati, “Ine ndiri ndi Lemba limene likukuwonetsani inu kuti Mpingo uli mu nthawi ya Chisautso.”

Ine ndinati, “Kawerengeni Chisindikizo cha Chisanu Ndi Chimodzi, ndizo zonse, iwo uli pomwe apo pansi pa nthawi ya Chisautso. Koma fufuzani, basi izo zisanachitike, Mkwatibwi adzakhala atapita kale. Mukuona? Iye ali mu Ulemelero pa nthawi imeneyo. Iye ali alibe kuyeretsedwa.” Mukuona?

“Iye amene akhulupirira pa Ine ali nawo Moyo wosatha, ndipo sadzafika poweruzidwa kapena Chiweruzo, koma wadutsa kuchoka ku imfa wapita ku Moyo.” Khristu anapereka lonjezo lakuti ife sitidzaima konse pa Chiweruzo. Kotero mwaulere Iye anatenga malo anga, mpaka kuti ndine mfulu kwathunthu. Pamene ine ndakhululukidwa, ine ndakhululukidwa. Kodi Iye angandichotsemo bwanji ine mu

shopu ya pinyolo, ndiri ndi lisiti labwino bwino, ngati... Zingatheke bwanji kuti Iye ndi Muomboli wanga, ndipo wandichotsamo ine mu shopu ya pinyolo, ndipo wogulitsayo nkumanenabe kuti ndine wake? Ine ndiri ndi lisiti lochita kulembedwa, ameni, mwaona, lolembedwa ndi Magazi a Yesu Khristu. Mukuona? Tsopano, zimenezo, apa ndi pamene ife tafika.

Iye anati, “Tsopano, inu mumutenga chotani, mumulekanitsa chotani Mkwatibwi wosankhidwa uja yemwe inu mukumukamba tsopano, inu muziika motani Izo pansi pa choimira?”

⁵⁷ Ine ndinati, “Mwakhoza.” Ine ndinati, “Ndi izi apa. Tsopano, mu Mateyu, mutu wa 27 ndi ndime ya 51.” Ngati ife... .

Mundilore ine ndingowerenga izi, ndiyeno ife—ife tizimvetsa izo bwino bwino. Ndiye ife tipeza ngati izo zinafaniziridwa kapena ayi, ngati ali Mkwatibwi wosankhidwa. Mateyu, mutu wa 27 ndi—ndi ndime ya 51. Chabwino. Ife tikuwerenga izi, pa kupachikidwa kwa Ambuye wathu.

Ndipo, taonani, chophimba cha mkachisi chinang’ambika pakati kuyambira pamwamba mpaka pansi;...

⁵⁸ Tsopano, limenelo linali lamulo. Lamulo linathera pomwepo. Chifukwa, chophimbacho chimawalekanitsa osonkhana ku zipangizo zopatulika za Mulungu. Wansembe yekha wodzodzedwa amakalowa kumeneko, ndipo, izo, kamodzi pa chaka. Mukukumbukira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, Mulungu, ndi dzanja Lake Lomwe, zindikirani, “kuyambira pamwamba mpaka pansi,” osati kuyambira pansi kupita pamwamba. Ndi mapazi forte ena muutali. Zindikirani, osati kuyambira pansi kupita pamwamba, koma “kuyambira pamwamba kupita pansi,” kuwonetsera kuti izo anachita ndi Mulungu. Anang’amba chophimbacho pawiri, ndiye ngakhale, aliyense, aliyense wofuna, akhoza kubwera ndi kudzatenga za chihero Chake. Mukuona? Chabwino.

...kuyambira pamwamba mpaka pansi; ndipo dziko linachita chivomezi, ndipo miyala inang’aluka;

Ndipo manda anatseguka; ndipo matupi ambiri a oyera amene anagona anauka,

Ndipo anatulukuka mmanda chitachitika chiukitsiro chake,... anapita mu mzinda woyera, ndipo anakawonekera kwa ambiri.

⁵⁹ Ndi amenewo Osankhidwawo, Mkwatibwi uja. Si mpingo wonse wa Chiyuda kuti unatulukira pa nthawi imeneyo. Onse a iwo ankapanga nsembe yofanana. Onse a iwo anali pansi pa mwazi wokhetsedwa wa mwanawankhosa. Koma panali Gulu losankhidwa; ndipo Gulu losankhidwa limenelo, mwamsanga

pamene chochitikacho chinabwera, limene linakhulupirira kwenikweni Izo ndi mowona mtima. Tsopano ine ndikubwera ku mawu akuti *kugonjetsa*. Tsopano sungani chimenecho. Awa amene anali atagonjetsa kwenikweni, moona mtima akumapanga chopereka chomwecho chimene ena onse a iwo amapanga, koma, moona mtima, anagonjetsa zinthu za mdziko. Pamene chitetezero chinapangidwira molondola pa iwo, iwo anali mu paradiso kufikira sewero lija pa nthawi imeneyo. Pamene nthawi imeneyo inapangidwa, iwo anali atagonjetsa ndipo anali akupuma, akugona; mwaona, “matupi aambiri a iwo amene anagona mu fumbi,” mwaona, amagona.

⁶⁰ Tsopano, ngati ife tikanakhala ndi nthawi, ife tikanabwerera mmbuyo kwa Daniele, pamene, Daniele, wosankhidwa uja amene anali atagonjetsa. Ndipo Iye anati, “Tsekera Bukhulo, Daniele, pakuti iwe udzapuma pamalo ako. Koma pamene Kalonga adzabwera, amene adzaimirire anthu, iwe udzaima pamalo amenewo.” Ndi izi apa. Daniele, mneneri uyu wa Mulungu, anawona nthawi yakumapeto ikubwera. Ndipo Iye anati, “Daniele, iwe udzaima pamalo ako pa tsiku limenelo.” Ndipo apa iye anali, atabwera; osati Israeli yense, koma woimira-Mkwatibwi wa Israeli. Tsopano, Israeli yense sakutulukira mpaka chiukitsiro cha aliyense.

⁶¹ Ndipo tsopano, pa Kubwera kwa Ambuye Yesu, iwo amene akukukonda kwenikweni Kubwera Kwake, ndi amene akukukhalira moyo iko; pamene Iye adzawonekera mu mlengalenga, Mpingo umene unafa mwa Khristu udzauka, ndipo iwowo adzasinthidwa mkamphindi. Ena onse a iwo sadzadziwa kalikonse ka izo. Kumbukirani, “Anawonekera kwa iwo mu mzinda.” Mukuona? A—a—Mkwatulo udzakhala monga chomwecho. Ife tidzawonana wina ndi mzake, ndipo ife tidzawawona iwo. Dziko lonse silidzawawona iwo. Iwo adzakwatulidwa ngati kupita kwa chinsinsi. Tikudikirira nthawi imeneyo!

Kenako nkudzabwerera padziko lapansi ku chisangalalo cha Zakachikwi chija, kenako zaka chikwi... “Akufa onse sanakhale moyo kwa zaka chikwi.”

⁶² Ndipo kenako nkudzatulukira mchiukitsiro cha aliyense, kumeneko, Israeli yense. Ndiponso, taonani apo, atumwi khumi ndi awiri, mbadwa khumi ndi ziwiri, onse akuimiridwa. Ndipo ife sitinafikebe kwa izo panobe. Mwinamwake, Ambuye akalola, ife tidzafika kwa izo mu Chipangano, mmene kuti makoma a yaspi aja, ndi miyala khumi ndi iwiri, zipata khumi ndi ziwiri, maziko khumi ndi awiri, zonse zomwe zikuimiridwa. Apa iwo ali pa mipando khumi ndi iwiri, angelo-atumiki a masiku amenewo, kuti akapereke chiweruzo pa iwo amene anakana uthenga wawo. Amen. Apo pakubwera ora lalikulu lija. Eya.

⁶³ Ndi tsiku bwanji, ndi nthawi bwanji imene ife tiri nkukhalamo! Mmene ife tiyenera kufufuza, Mpingo. Tsopano ife timakamba za zinthu izi kuti zikubwera, zimene ziti zidzabwere. Tsopano, lero, tiyeni tibwerere mmbuyo apa ndipo tiwone, tidzifufuze tokha ndipo tiwone ngati ife tiridi mu Chikhulupiriro.

⁶⁴ Tsopano tiyeni tiyankhule za agonjetsi ochepa kwa mphindi pang'ono, mmasiku a nthawi ya Nowa, imene inafaniziridwa ndi Yesu Khristu, kuti inali monga lero.

Ine ndikuyenera kukhala ndi maminiti teni. Tsopano ine ndikhala theka la ora. Ine ndikungoyamba kumene, tsamba loyamba. Ine ndilumpha pang'ono a iwo, ngati ine ndingathe. Ndi kutenga chimene. . .

⁶⁵ Mu nthawi ya Nowa, choimira cha lero: Yesu analozera kwa izo, ndipo anati, “Monga izo zinali mu nthawi ya Nowa, chomwechonso zidzakhala pa Kudza kwa Mwana wa munthu. Mu nthawi ya Nowa, zidzakhalsoso chomwecho mu Kudza kwa Mwana wa munthu.” Zindikirani, apo panali dziko lachigumula lonse lija, mwinamwake mamillioni a anthu, analipo agonjetsi eyiti. Anthu eyiti anagonjetsa, amene anali enieni, agonjetsi enieni. Kunali ana aamuna atatu a Nowa ndi azikazi awo, ndi Nowa ndi mkazi wake. Eyiti anagonjetsa, amene anakalowa mu chombo pa nthawi yoikika. Kodi iwo anachita motani izo? Iwo amamvetsera Mawu a Mulungu. Iwo sanapezeke ali panja pa chitseko. Iwo anapezeka mkati mwa chitseko.

⁶⁶ Oh, abwenzi anga okonedwa, musalole chitseko chimenecho chitsekedwe. Yesu anati, “Monga izo zinali mu tsiku limenelo, chomwechonso izo zidzakhala pa Kudza kwa Mwana wa munthu.” (Zikomo inu, m'bale.) “Chomwechonso zidzakhala pa Kudza kwa Mwana wa munthu.” Tsopano, pali wina ati adzapezeke ali panja pa chitseko.

Ambiri a iwo mwina anali ndi zolinga zabwino, ndipo, “Tsiku lina, ngati zinthu zoterozo zidzachitika, ife tidzakalowa ndi M'bale Nowa, chifukwa iye ndi munthu wabwino.” Koma, inu mukuona, izo zinangotengera mkati eyiti okha.

⁶⁷ Tsopano, muganize zolimba tsopano. Ngati inu mukungogona, kumakhala olekelera, lowani mkati. Fulumirani, msanga, chifukwa chitseko chikhoza kutsekedwa nthawi iliyonse.

⁶⁸ Ndipo nthawizonse kwakhala kuli chombo mu chuma cha Mulungu. Kunali chombo mmasiku a Nowa, chopulumukira anthu Ake. Kunali likasa mmasiku a lamulo, likasa la umboni. Mmasiku a lamulo, iwo ankatsatira likasa.

Ndipo pali m'badwo wachitatu tsopano; monga nthawi ya Nowa, nthawi ya Loti, ndipo tsopano nthawi ino. Pali chombo tsopano. Ndipo chombo chimenecho si chipembedzo, komanso si ntchito zabwino zimene iwe ukuchita. Ichu ndi

“mwa Mzimu umodzi,” Aroma 8:1, “ife tonse timabatizidwira kulowa mu Thupi limodzi, mu zochitika za Ufumu umenewo, ubatizo umodzi Wauzimu.” Ziribe kanthu kaya ndiwe wabwino bwanji, woyipa bwanji, chirichonsecho, umalowa mu Ufumu umenewo mwa—mwa ubatizo wa Mzimu Woyera. Mukuona? Ndiyo njira yokhayo imene iwe umagonjetsera. Ndi onse omwe ali pansi pa Magazi okhetsedwa omwe ali agonjetsi, chifukwa iwe sungagonjetse, pawekha. Ndi Iye amene amakugonjetsera iwe. Iwe ukupuma.

⁶⁹ “Kodi ine ndidzadziwa bwanji ndiye, M’bale Branham, kuti ine ndiri Mkatimo?” Muwone mtundu wa moyo umene inu mukukhala. Mungoyang’ana pokuzungulirani. Mungoona ngati iwo ukungokhalidwa mwa inu, mosadzipangitsa. Kapena, kodi inu mumachita kulimbana nazo ndi kukokerera, mwaona, zikatero inu mukuchita izo. Koma musamayesere kuti muzichita izo. Kodi inu munayamba mwayeserapo? Eya. Musamatero.

⁷⁰ Ziri ngati kuika nkono wa mwana wamng’ono mu nkono wa malaya, inu mukuona. Iwo umangokhwepa, khwepa, mmenemo, ndi china chirichonse. Mukuona? Iye sangathe kuchita izo. “Vala chikhotho chako, wokondedwa.” Iye sangathe kuchita izo. Nkono waung’onowo ukungokhwepa, khwepa, mozungulira. Zimatengera dzanja lako lokhazikika.

Oh, ndine wokondwa bwanji, ine ndikhoza kungopereka dzanja langa kwa Atate, ndikuti, “Ambuye Yesu, ine ndikulephera kufika Mmenemo. Inu mundithandize ine. Mundiveke ine chikhothocho.” Ine ndasiya kumayesera. Ingomusiyani Iye kuti azichita izo. Mukuona?

⁷¹ Ngati mwana wamng’ono apitiriza kumayesera, “Oh, ine nditha kuchita izo. Ine nditha kuchita izo.” Ndipo iye akungopezeka paliponse. Iye sangathe kuchita zimenezo.

Inunso simungathe, inenso sindingathe, koma ngati ife titagwiritsa ndi kumulola Iye kuti azichita izo. Kungodzipereka kwa Iye, “Apa, Ambuye, ndine ndiri pano. Basi—mungondisiya ine ndisakhale kanthu. Ine—ine ndikudzipereka. Inu muyike dzanja langa pa malo oyenera.” Ndicho chigonjetso. Ndiko kugonjetsa.

⁷² Chinthu chimene inu mukuyenera kuchigonjetsa ndi inueni, maganizo anu, chinthu chanu, ndipo mudzipereke nokha kwa Iye. Iye anakugonjetsarani inu. Iye amaidziwa njirayo; ife sitikuidziwa.

⁷³ Koma mu nthawi ya Nowa analipo agonjetsi eyiti, ndipo awo ndi amene anakalowa. Iwo anagwiridwira mkati.

Tsopano taonani, abwenzi. Ine ndikukhulupirira iwo akujambula izi. Ndipo ngati izo ziri pa kanema, kapena osati tele... mundikhulukire ine, tepi. Chirichonse chimene inu mukuchita, amene akumvetsera tsopano, kapena amene ati adzamvetsere zikatha pano, ora latha kwambiri, ndipo

inu muli ndi cholinga chabwino, koma mugwiridwire mkati. Tsopano, musalimbane nazo. “Si iye amene afuna, kapena iye amene athamanga, koma Mulungu.” Mungomusiya Mulungu. Mungodzipereka nokha kwa Iye ndi kumapitirira kuyenda, ndi chikhulupiriro changwiro, chokhutitsidwa, kuti, “Chimene Mulungu analonjeza Iye ndi wokhoza kuchichita.” Osati kujowina chipembedzo chimodzi, chipembedzo china, kuthamangira *izi, izo*, kapena *zinazo*, kuyesera *izi*. Ingodziperekani nokha kwa Mulungu, ndipo muziyenda ndi Iye, mwamtendere, mwakachetechete, mosasokonezedwa. Ingopitirirani kumayenda ndi Iye. Uko nkulondola.

⁷⁴ Ndicho chimene ine ndinamuza m’bale wathu amene anali a—zinamusokonekera. Mukuona? “Ingodziperekani kwa Iye. Iye ali pano, Iye Amene akudziwa zimene inu mwachita, ndi chimene chinapangitsa kuti inuyo mudzakhalepo ndi kumachita mwanjira *iyi*, ndi zonse izo. Iye amadziwa zonse za inu, ndipo tsopano Iye wangokuuzani inu choti muchite. Tsopano,” ine ndinati, “chinthu chokhacho chimene inu muyenera kuchita ndichakuti mungopita mukachite izo. Kachitidwe kake, mukaiwale zonse za kale, muzikayenda, muzikakhalira moyo zamtsogolo, mu Ulemelero ndi Pamaso pa Mulungu.”

Agonjetsi eyiti.

⁷⁵ Mmasiku a nthawi ya Daniele, kunali agonjetsi foro amene anakhoza kuima yesero la moto ndi mkango.

Tsopano, ife timayembekezedwa kuti tidziyesedwa. Ilo ndi phunziro labwino kwa wanga—m’bale wanga kumbuyo uko, nayenso. “Iye amene adza kwa Mulungu ayenera poyamba ayesedwe.” Kuyesedwa (ndi chiyani?) ndi Mawu. Ndiko kuyesa kwa Mulungu. Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] “Iye amene adza kwa Mulungu ayenera kuyesedwa.” Izo zimangowonetsera mwana weniweni, kenako, mwaona, kuyesedwa. Ndipo pamene yesero libwera. . . Iwe sungagonjetse pokhapokhapo ngati pali yesero laperekedwa kwa iwe. Ndipo pamene yesero liperekedwa, ndi lakuti awone ngati iwe ugonjetsa kapena ayi. Ndipo Yesu anati, “Kwa iye amene agonjetsa,” yeserolo. Yesero ndi chinthu chachikulu chimene chinayamba chachitikapo kwa iwe. Ine ndikukhulupirira izo zinalembedwa mu Lemba, Petro ananena, kuti, “Mayesero athu ndi oyenera mochuluka kwa ife kuposa golide wantengo.” Ndi nthawi yoyesedwa. Iwo ndi umboni umodzi wabwino kwa ife kuti Mulungu ali ndi ife, pamene ife tiyesedwa, pakuti ana onse a Mulungu amayesedwa ndi kuyezedwa.

⁷⁶ Ndipo Daniele, mwamuma, mneneri; Shadreki; Misheki; ndi Abedinego; Daniele anali mneneri; ndipo uwo unali usinkhu wa Mpingo mu tsiku limenelo, ine ndikutanthauza, Mkwatibwi. Pali mipingo yambiri, pafupifupi thuu milioni a

iwo anapita kumeneko. Koma uko kunali . . . Uwo unali usinkhu wa mgonjetsi. Ndipo agonjetsi amenewo anaikidwa pa yesero. Ndipo mgonjetsi aliyense amayenera kuikidwa payesero. Ndipo pamene iwo anati, “Inu mubweze chimene Mawu akunena, kapena muponyedwa mu ng’anjo ya moto,” iwo anakana chirichonse koma Mawu.

⁷⁷ Ndipo pamene Daniele anapatsidwa yesero, kuti abweze chimene Mawu ananena, kuti iwo azitsamira moyang’ana ku kachisi, monga Solomoni anapempherera, ndipo Iye adzawapulumutsa iwo ku zinthu zonse. Mulungu akanadzamva kuchokera Kumwamba ngati iwo akanadzatsamira . . . akadzayang’ana molunjika ku kachisi ndi kupemphera. Ndipo anati, “Ngati munthu aliyense adzapemphera masiku akuti . . . Ndipo ife ndi a Medo-Persia, amene sitimasintha kapena kuwakonza malamulo athu. Munthu ameneyo adzaponyedwa mu dzenje la mikango.”

⁷⁸ Iwo anamtchera msampha iye. Ine ndikukhulupirira kuti mneneri ameneyo amadziwa zimenezo. Koma iwo anamtchera iye msampha. Iye anayenda modzichepetsa. Pamene inafika nthawi yoti iye apemphere . . . Nthawi imeneyo, iye amadziwa, kwawo ku Yerusalemu, kunali nsembe imawotchedwa pa guwa. Daniele samawawopa akazitape awo. Anakwezera mmwamba makatani, ndipo anaponyera mmbuyo zotchingira, ndipo anagwada pansu pa mawondo ake, ndipo anakwezera manja ake mmwamba kwa Mulungu ndipo anapemphera. Bwanji? Moyo kapena imfa, iye anali ndi chigonjetso. Ndipo, chotero, chigonjetso chochuluka kwambiri mpaka mikango siinathe kuwadya iwo. Iye—iye anagonjetsa.

⁷⁹ A . . . Shadrecki, Misheki, Abedinego anali ndi chigonjetso chochuluka mpaka mkango . . . mpaka moto sunathe kuwawotcha iwo. Inu mukudziwa, chigonjetso ndi chinthu chovuta kuchiwocha, kapena kuchidya, kapena chirichonse. Mukuona? Chotero, iwo, iwo anali nacho icho.

⁸⁰ Ine ndikhoza kutchula munthu wina. Mmasiku a Loti, Yesu ananena za izo, kunali atatu okha amene anagonjetsa, Loti ndi ana ake aakazi awiri. Osati ngakhale mkazi wake; sanagonjetse. Iye—iye ananyamuka nawo. Iye ndi choimira. Ndikanakonda ife tikanakhala ndi nthawi. Maminiti sate anga atha tsopano. Mukuona? Mukuona? Iye, iye anachita zabwino, iye ananyamuka.

⁸¹ Tsopano ine ndiyenera kupereka ichi kwa inu, mphindi chabe. Ambiri a inu munanyamuka, inunso. Ambiri a inu munazisiya zinthu izi, kuti mudzatenge maimidwe anu, inu mutatha kuzifufuza Izo kudutsa Lemba ndipo munadzapeza kuti Izo ndi zolondola. Inu munawona kutsimikiziridwa kwa Mulungu Wamphamvuzonse; osati ndi ena, zimene winawake *ananena* kukhala chitsimikizo. Chimene Baibulo linati

chikanadzakhala, ndipo apa Icho chikuchita izo. Inu munawona kuti Icho chinali Choonadi. Kotero, inu mwakonzeka, kuti muchoke ku Sodomu, muchoke ku chipembedzo, muzisiye zinthu zokumangirirani inu ku kachikhulupiriro; ndi kuti mumutsatire Khristu, mwa Mzimu Woyera akudzitsimikizira Yekha mwa Mawu olembedwa a Mulungu. Mwa kulankhula kwina, inu munatenga Baibulo m'malo mwa kachikhulupiriro. Inu mwayambapo, kuti muzimutsatira.

⁸² Chabwino, mkazi wa Loti anachita chinthu chomwecho, inu mukudziwa. Iye ananyamuka, kuti azipita ndi Loti, kumutsatira mwamuna wake, ana ake, okonedwa ake, koma Izo munalibemo mu mtima mwake. Iye amalikondabe dziko lapansi. Kotero ndi zotheka kuti iwe ukhoza kuyambapo, ndipo komabe ndi kukhala nalobe dziko mwa iwe. Mukuona? Iye sanagonjetse nkomwe. Ndipo ngakhale anali kale pa msewu, izo potsiriza zinamuchotsapo iye. Iye amafuna kuyang'ana kumodzi kwakukulu, kotalika, kotsiriza kuja. Apo ndi pamene iye anakodwera. Musati muziyang'ana m'mbuyo mpang'ono pomwe. Musamakhale ndi zokhumba. Muzingopitirira kumayenda. Muike malingaliro anu pa Kalvare ndipo mukhale mukuyendabe kupita kwa Khristu. Mukuona?

⁸³ Iye anauyamba, ngati m'gonjetsi, koma iye sanagonjetse konse. Oh, iye anasiya chipembedzo. Iye anatero. Iye anatuluka kuchoka mu Sodomu, ndi Loti. Koma iye ankafuna kuti abwererenso kuti azikadula tsitsi lake. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Mukuona? Iye ankayenera kuti abwererenso. Iye sakanakwanitsa basi kupirira nalo—yesero. Iye ankayenera kuti ayang'anenso mmbuyo, kuti awone zomwe ena onse a iwo anali kuchita. “Oh, inu mukudziwa, ine ndinali ndi abwenzi ena abwino kumusi uko, ndiponso. Ndipo, kuwonjezera apo, izi zikhoza kungokhala pang'ono chabe—kusuntha kwakung'ono. Ine sindikudziwa ngati zingakhale zolondola kapena ayi. Ine—ine ndangotenga mawu a munthu uyu a izo, ngakhale iye ali mwamuna wanga. Komabe. . .” Abusa ako ndi amuna ako, kuyankhula mwauzimu, inu mukuona. “Tsopano, kaya ndi zoon kapena ayi, ine sindikudziwa. Mwinamwake iye, vumbulutso lake si loona.”

Ndiye, ngati iwe sukukhutsidwa mwangwirowi, iwe sukudziwa mwangwirowi kuti Izo ndi Mawu a Mulungu, ndiye—ndiye iwe sungathe kupita. Mukuona? Iwe uyenera kukhala wogulitsidwa kwenikweni. Iwe uyenera kuti uzidziwa. Osangonena kuti, “Chabwino, ine ndawona ena akuchita izo. Ine ndawona chizindikiro.”

⁸⁴ Inu mukudziwa, Israeli anawuyamba, ine ndikhoza kunena chinthu chomwecho ndi kuchibweretsa icho pano. Iwo anauyamba, thuu milioni amphamvu, ndipo anadzatsirizira ndi amuna awiri. Kulondola. Iwo anawona ntchito za Mulungu. Iwo anawona mawonetseredwe a Mzimu. Iwo anawona,

zozizwitsa zazikulu zamphamvu zikuchitidwa uko ku Igupto, ndi chirichonse, ndipo anauyambapo. Koma izo—izo sizinali mu mtima mwawo. Iwo sanagonjetse. Iwo anangotuluka. Ndipo Yesu anati, “Ndipo iwo anafera mu chipululu,” ndipo anafa Mwamuyaya. “Mmodzi aliyense wa iwo anafa,” izo zikutanthauza kusiyana Kwamuyaya. Mmodzi aliyense wa iwo anavundira mu chipululu.

⁸⁵ Koma kunali amuna awiri, Yoswa ndi Kalebu. Ndipo pamene izo zinadzafika pa chiwonetsero, zolepheretsa zinali zazikulu kwambiri mpaka iwo anawoneka ngati ziwala kumbali ya iwo. Yoswa anafuula ndi Kalebu, ndipo anati, “Ife ndi okhoza kuchita izo.” Bwanji? “Mulungu wanena chomwecho.” Ndipo iwo anali agonjetsi. Iwo anagonjetsa. Iwo anali iwowo amene anachita mwayi, kuchokera pa mgwirizano wonse wawukulu wa anthu uja, anatenga Mkwatibwi, weniweni wosankhidwa kupita naye ku dziko lolonjezedwa. Yoswa ndi Kalebu pa mzere wapatsogolo kunja uko, ngati akulu ankhondo awiri, anawatsogolera iwo mpaka pa mtsinje, ndipo anawoloka mtsinjewo, anapita ku dziko lolonjezedwa. Chifukwa chiyani? Iwo anakhulupirira Mawu, zinalibe kanthu kuti zinali chiyani.

⁸⁶ Kenako, anauka Datani. Datani, kani, anauka, ndipo chomwechonso Korah, ndipo iwo anayesera kunena kuti, “Munthu uyū akuyesera kudzipanga yekha wapamwamba pa ife tonse; iye ndi woyera kwambiri kuposa ena onse a iwo.” Mulungu atatha kumutsimikizira kwathunthu munthuyo. Iwo anati, “Ife tingoyambitsa gulu la anthu ndipo ife tipanga *ichi, icho*, kapena *china*, ndipo ife tipanga mabungwe athu, ife titero. . .” Ndipo iwo anafa ndipo anawonongedwa.

Koma amuna amenewo anali ndi Mawu aja a Ambuye, ndipo iwo anakhala ndi Iwo, ndipo iwo anakawoloka.

“Si iye amene amayamba; iye amene amamalidzitsa.” Ambiri amayamba liwiro, koma pamakhala Mmodzi amene amakamalidzitsa iwo. Padzakhala matchalitchi ambiri oyamba, magulu ambiri a anthu. Padzakhala Gulu limodzi lidzamalidzitse. Amenewo ndiye agonjetsi.

⁸⁷ Tsiku la Loti, inde, iye ankeyenera kukhala ndi kuyang’ana mmbuyo kumodzi, kotalika kuja. “Oh, ine ndikumusiya *Wakuti-ndi-wakuti* kumusi uko, nthawi zabwino zija zimene ife timakhala nazo. Ine sindidzaiwala konse izo.” Ndipo iye anagwidwa, anatekeredwa panja, monga izo zinali mmasiku a Nowa. Iye anatekeredwa panja, popanda chifundo, ndipo iye anafa. Ndipo chu—chulucho chikadali uko mpaka lero. Iwo amati (ine sindikudziwa) iwe ukhoza kunyema kachidutswa ka icho ndipo icho chimeranso, chipilala cha mchere. Inu mukadzachiwona chithunzi chija cha *Sodomu Ndi Gomorrah*, inu mudzawona chipilala chenicheni cha mchere chimene chinaima kumeneko.

⁸⁸ Tsopano, pali kusiyana pakati pa chipilala cha mchere ndi Lawi la Moto. Mukuona? Iwe uyenera kutembenukira mbali imodzi. Eya.

⁸⁹ Zindikirani, mu nthawi ya Yohane M'batizi. Mu nthawi ya Yohane M'batizi, kunapezeka sikisi amene anagonjetsa. Mibadwo yonse, iwo akhala ali nawo agonjetsi. Mu nthawi ya Yohane anali nawo sikisi, amenewo anali Yosefe ndi Maria, Zakariya ndi Elizabeti, Simioni ndi Anna. Mwamuna ndi mkazi, mwamuna ndi mkazi, mwamuna ndi mkazi; mwaona, choimira Khristu, Mpingo; Khristu, Mpingo; Khristu, Mpingo; Khristu, Mpingo. Mukuona? Mukuona?

⁹⁰ Zindikirani, izo zimayambira kwa munthu wachirengedwe. Ayi, Mo-. . . Yosefe, munthu wachirengedwe, Yosefe, anali chiyani iye? Kalipentara. Kenako wansembe, anali chiyani iye, mukuona? Mtumiki mu nyumba ya Ambuye; Zakariya. Ndipo kuchokera kumeneko, kupita kwa Simioni, mneneri ndi mneneri wa mkazi. Mukuona? . . .? . . . Kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera. Ameni. Kodi inu simukuziwona izo? [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Mwangwiro. Sikisi anagonjetsa. Ena onse a iwo, amapereka nsembe yawo ndi chirichonse, koma awa anali Osankhidwa. Iwo anagonjetsa.

⁹¹ Zindikirani m'badwo wa mpingo uliwonse. Omwewo amagonjetsa pamene iwo, mwana wamwamuna aliyense kuchokera mu m'badwo wa mpingo uliwonse, akagonjetsa yesero la m'badwo umenewo. Ine ndiri nawo Malemba apa. Ine sindikuganiza kuti ife tiri nayo nthawi kwenikweni kuti tipange izo, koma ife tikudziwa uliwonse wa mibadwo ya mpingo. Chimodzimodzi tsopano. Izo ziri ngati winawake amene ali . . .

⁹² Mwaona, monga ine ndinanena poyambirira, iwe umabadwa wogonjetsedwa. Ndipo kubadwa kumeneko sikungakubweretse iwe ku—ku Moyo, chifukwa iwe umabadwa wogonjetsedwa. Ndipo iwe umadzakhala mu dziko logonjetsedwa, pakati pa anthu ogonjetsedwa, pakati pa tizikhulupiriro togonjetsedwa, zipembedzo zogonjetsedwa. Iwe umayenera kubwera ku chigonjetso mwanjira inayake.

⁹³ Izo ziri chimodzimodzi ngati kakombo. Kumene ama. . . Kakombo, ine ndikuganiza, ndi limodzi la maluwa okongoletsetsa amene alipo. Ine ndimakonda kwambiri kakombo wa calla wopambana uja ndi kakombo wa mudziwe. Ine ndikuganiza palibe chirichonse chokongola ngati kakombo wamkulu wa mudziwe, mumamutcha iye kakombo wa mmadzi. Mmene iye amawonekera! Tsopano, kodi iye amachokera kuti? Iye amakhala kambewu kakang'ono, pansi kupansi kwa dziwe la matope, lonyansa. Ndipo kambewu kakang'ono ako, apobe, kukongola konse kumene kuti kudzawale mwa iye, kumakhala mwa iye nthawi imeneyo, pamene iye ali mmatope amenewo. Koma iye amayenera kumenyera, tsiku ndi tsiku, podziwa kuti

pali chinachake. Mumakhala mwakuda. Mumakhala monyasa. Mumakhala mwamatope. Mumakhala mwaziphala zathope. Mu ziphala zathope izo zimene iye akukhalamo, komabe amamenyera njira yake kudutsa mu thopelo, monyansa, ndi madzi, ndi malo okhathamira, mpaka ilo limatulutsa mutu wake pamwamba, mu kuwala, ndi kuwonetsera chimene chinabisidwa mwa iye nthawi yonseyo.

⁹⁴ Ine ndikuganiza ameneyo ndiye mgonjetsi, amene, nthawiina anali mu tchimo, nthawiina ankachita zinthu zimene zinali zolakwika, musadandaule za izo tsopano. Nthawiina ankachita zinthu zimene zinali zolakwika, ndiye, tsopano muyang'aniranji mmbuyo mu dziwe kachiwiri? Mukuona? Onani, inu muli . . .

⁹⁵ Mulungu, mwa kukonzedweratu Kwake, mwaona, anaibweretsa mbewu iyi ku moyo, ndipo iyo ikudzikankha yokha, mwaona, kubwera ku kuwala. Ndipo tsopano, pamwamba pa zonse izo, iyo yagonjetsa. Mukuona? Iyo siimadziwonetsera yokha pansu apo. Iyo ikudzuka, kuti idzadziwonetsere yokha.

Inunso simunatero, mu lanu—tchimo lanu, ndi chigololo, ndi chirichonse chimene inu mmakhalamo. Inu simunkawonetsera chirichonse. Koma inalipo mbewu mmenemo, ndipo iyo inapeza mwayi woti idzikankhire yokha mu Kuwala. Ndipo tsopano inu muli mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, ndi Kuwala kwa Mwana. Izo zinatulutsa chimene inu munali kwenikweni pachiyambi. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Inu munakuwona Kuwala. Inu munabiriwira. Inu munawutsegula mtima wanu, ndipo tsopano ndinu kakombo.

⁹⁶ Inu mukukumbukira ulaliki wanga wa kakombo? M'busa Kakombo, mmene iye amavutikira. "Ndipo, komabe, kodi iye samadzipota. Ndipo komabe, Solomoni, mu ulemelero wake wonse, sanavekedwe monga m'modzi wa awa." Iye—iye—iye—iye—iye . . . Tayang'anani pa iye. Iye amakhala wokonzeka kuti ape . . . Iye samadzitengera yekha kalikonse. Kakombo samalabadira kalikonse ka iyemwini. Kodi iye amachita chiyani? Iye—iye amaponyera kukongola kwake panja, moyo wake, kuti ena athe kuwuwona. Moyo wake umawonetseredwa panja, kuti ena akathe kuwona ulemelero, chomwe chiri mwa iye, chimene chinali mwa iye mmatope amenewo. Tsopano iye ali pamwamba.

Ameneyo ndiye m'gonjetsi. Iye wagonjetsa matope. Iye wagonjetsa zinthu za mdziko. Ndipo tsopano iye mwaulere akudzipereka yekha. Aliyense akhoza kumuyang'ana iye. Moyo wake, inu simungathe kuloza chala pa iye. Mukuona? Iye ndi m'gonjetsi weniweni. Inu simungathe kunena kanthu za iye tsopano. Kutu, "Iye anatuluka mmatope." Koma iye sali m'matope tsopano. Iye ali pamwamba pa iwo. Ameni. Inu tsopano simungaloze mmbuyo chimene iye anali. Iye ndi chiyani tsopano? Iye ali pamwamba.

97 Kenako njuchi zimabwerapo ndikuti, “Amenewo ndi mafuta onunkhira abwino. Ndikukhulupirira ndipita ndipo ndikatenga gawo langa.”

98 Iye amangodzitsegula mtima wake, “Kazibwerani tsopano. Chabwino.” Chirichonse chimatenga kuchokera mwa iye. Mukuona? Iye, iye ndi m’busa weniweni. Iye amawonetsera Ulemelero wa Mulungu. Ndipo taonani kumene iye akuchokera. Iye anachita kugonjetsa, kuti achite zimenezo.

99 Nthawi ina, mwamunayo kapena mkaziyo anali wamng’ono ndi wowoneka bwino, wokongola. Iwo anali ndi mayesero ambiri oti adutsemo, koma iwo anagonjetsa izo. Mukuona? Iwo anagonjetsa. Tsopano iwo akuwonetsera kukongola kwenikweni kwa Khristu m’moyo wawo. Zindikirani, kuwonetsera, kudutsa mmatope.

100 Yesu anatipatsa ife chitsanzo, mmene tingachitire izo. Tsopano ife tikufuna kudziwa mmene tingagonjetsere. Yesu anatiuza ife mmene tingachitire izo. Mukuona? Kudzichepetsa! Anadzimangira Yekha, anatenga chopukutira, ndipo anasambitsa mapazi a ophunzira ndipo anawapukuta iwo. Mulungu yemweyo wa Kumwamba anadzichepetsa Yekha.

101 Ife sitimafuna kuti tichepetsedwe. Ndicho chifukwa chake akazi samafuna kuti tsitsi lawo lizikula (Mukuona?); nchifukwa chimene iwo samafuna kuvala monga madona ayenera kuvalira. Monga, amuna samafuna kutero, mwaona, ndi chinthu chomwe chomwecho. Iwo samafuna. Iwo, iwo amanyozeka.

Koma, Yesu, kawirikawiri! Penyani Yemwe Iye anali. Ukulu! Ine ndinena chinachake. Ukulu umadzichepetsa wokha. *Ukulu* umadzichepetsa wokha. Ukulu!

102 Ine ndakhalapo nawo mwayi wopeza, wokumana ndi anthu ena otchuka. Ndipo ndi anthu awa amene amakhala ndi tizovala tosinthira, ndi masenti fifite m’thumba mwawo, akuphokosera, uyo ndi munthu amene amaganiza kuti iye ndi winawake pamene iye si kanthu. Koma ine ndinaimapo pafupi ndi anthu otchuka, ine ndikutanthauza anthu otchuka okhala ndi malaya azigamba mmikono, mopindira. Iwo amakupangitsa iwe kumaganiza kuti ndiwe munthu wotchuka. Mukuona?

Ukulu ndi kudzichepetsa. Musaiwale zimenezo, Mpingo. Ukulu umafotokozedwa mu kudzichepetsa, osati mmene ungakhalire wabwino.

Ine sindikutanthauza kukhala wawutchisi, tsopano. Ine—ine ndikutanthauza wodzichepetsa mu mzimu. Mukuona? Ine sindikutanthauza kungotenga—kutuluka wosachapa ndi wosasamba. Izo, inu muzichita zimenezo. Inu mukudziwa zimenezo. Mukuona?

Koma ine ndikukamba za kudzichepetsa, kudzichepetsa kwenikweni, osati chinachake chongovala. Chinachake chimene chiri, uko ndiko kudzichepetsa kwenikweni.

¹⁰³ Yesu anatiuza ife mmene tingachitire izo. Iye anagonjetsa. Kutanthauza... *Kugonjetsa* kumatanthauza “kupambana yesero,” uko nkulondola, monga oyera onse akale ankachitira; monga Yesu anachitira: pakati pa adani Ake onse, Iye anapambana yesero. Chirichonse Iye amayesedwa nacho, Iye amapambana icho. Mu nkhope yomwe ya matenda, ndipo Iye pokhala Mesiya, Iye anawachiritisa iwo. Mu nkhope ya imfa, Iye anaibweretsanso iyo ku moyo. Mu nkhope ya Kalvare, imfa Yake Yomwe, Iye anaigonjetsa iyo podzipereka Yekha. Bwanji? Ndi Mawu. Anati, “Inu muwononge Kachisi uyu, ndipo ine ndidzamudzutsanso Iye mmasiku atatu.” Mawu ananena chomwecho. Mukuona? Ndipo pamaso pa imfa, Iye anaigonjetsa iyo. Iye anaigonjetsa imfa. Pamaso pa gehena, Iye anapambana gehena ndipo anagonjetsa gehena. Inde. Pamaso pa manda, Iye anawagonjetsa manda. Bwanji? Zonsezo mwa Mawu, ndi kudzichepetsa. Oh, mai! Ndi ameneyo Munthu weniweni. Ndi Uyo amene ayenera kupanga chitsanzo chanu. Mukuona? Iye anagonjetsa chirichonse, anagonjetsa izo.

¹⁰⁴ Taonani. Yesero linali la Iye. Inu mukudziwa zimenezo? Baibulo linati, “Iye anayesedwa mu nsonga zonse monga ife, komabe wopanda tchimo.” Iye anayesedwa ndi—ndi kumwa. Iye anayesedwa ndi akazi. Iye anayesedwa ndi chirichonse chimene akanayesedwa nacho. Iye anayesedwa ndi chirichonse chimene ife tiri. Iye anali Munthu, ndipo komabe iwe sukanaloza chala pa Iye. Inde, bwana.

¹⁰⁵ *Kugonjetsa* kumatanthauza “kumuzindikira mdierekezi mu iliyonse ya njomba zake.” Anthu ambiri amati, “Kulibeko mdierekezi. Ilo ndi lingaliro chabe.” Inu musamakhulupirire zimenezo. Alipo mdierekezi weniweni. Iye ndi weniweni basi monga inu muliri kapena aliyense. Mdierekezi weniweni, ndipo inu muyenera kumuzindikira iye kwenikweni. Inu muyenera kudziwa kuti iye ndi mdierekezi. Ndiye, nthawi yomweyo imene inu—inu mungamuzindikire iye, ndi kudziwa kuti iye ndi mdierekezi ndipo iye akulimbana ndi inu, ndiye, kuti mumugonjetse, inu mukuyenera kuzindikira kuti Mulungu mwa inu ndi wamkulu ndi wamphamvu kuposa mmene iye aliri, kuti Uyo amene ali mwa inu wamugonjetsa kale iye. Ndipo, mwa chisomo Chake, inu simuli woti mungafanizidwe ndi iye. Ameni. Apo pamakhala kugonjetsa kwenikweni, pamene inu mumuzindikira.

¹⁰⁶ Inu mumayang’ana mmbuyo, ndikuti, “Ine ndikuchita *ichi* ndipo ine ndikuchita *icho*,” zikatero, ayi, inu—inu, inu mwagonjetsedwa.

“Koma palibe kutsutsika kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu, amene sayenda monga mwa thupi, koma monga mwa Mzimu.” Zikatero iwe umazindikira kuti iwe wagonjetsa.

Ndipo iwe umadziwa kuti iye ndi mdierekezi. Iwe sunganene kuti, “Ine ndikudwala, ndipo ine—ine—ine—ine sindikukhulupirira kuti ndi nthenda.” Oh, inde, iyo ndi nthenda. Iwe uli ndi khansa, iwe “usakhulupirire kuti iyo ndi khansa.” Iyo ndi khansa. Iyo ndi khansa.

Koma, kumbukirani, “Wamkulu ndi Iye amene ali mwa inu kuposa iye amene ali mu dziko.” Iwe uyenera kuzindikira kuti Mzimu Woyera umene uli mwa iwe unagonjetsa kale chinthu ichi. Ndipo Iye ali mwa inu, ndipo inu mukhoza kugonjetsa mwa Iye. Izo ndithudi ndi zanzeru, ndizo ndendende mmene Lemba linalembedwera. Kugonjetsa!

Ine ndiyenera kuti ndifulumire. Ine ndatsala ndi maminiti forte-faifi tsopano. Ine ndithudi nthawi ikundithera tsopano.

¹⁰⁷ Zindikirani, kugonjetsa! Mulungu amene ali mwa inu ndi wamkulu kuposa amene ali mwa iye. Mulungu wa mdziko si wamkulu ngati Mulungu wa Kumwamba, amene ali mwa inu, palibe mdima wochuluka umene ungaimo mukupezeka kwa kuwala.

¹⁰⁸ Tsopano, mdima sungathe kuima mu kupezeka kwa kuwala. Ine sindikusamala kuti kuli mdima wotani, kuwala kuwuzimitsa iwo. Iwo siwungaimo. Ulemelero! Koma inu mutenge mdima wochuluka mmene inu mungafunire, ndipo mudzayesere kuima pafupi ndi kuwala nthawi ina, muwone zomwe zimachitika.

Uyo ndi Amene ali mwa inu, ndiye Kuwala. Ndipo amene ali mu dziko ndi mdima. Chotero, Kuwala kwatsimikizika kuti kumagonjetsa mdima, ndipo munthu amene ali mwa Khristu ndipo akudziwa kuti wagonjetsa zinthu za mdziko. Amen. Izo ziribenso chomangilira kwa iwe, nkomwe. Ndiwe mfulu. “Ukuyenda mu Kuwala, monga Iye ali mu Kuwala, ndipo Magazi a Yesu Khristu amatiyeretsa ife ku tchimo lonse, ndipo ife timakhala ndi chiyanjano wina ndi mzake.” Ndi zimenezotu.

¹⁰⁹ “Iye amene ali mwa inu ndi wamkulu kuposa iye amene ali mdziko.” Tsopano, ngati inu mmayang’ana mmbuyo ndipo inu nkumatsutsidwa, ndiye kuti inu mukadali mdziko. Koma ngati inu mukukhala pamwamba pa zimenezo, ndiye kuti Iye amene ali mwa inu wakutsogolerani inu pamwamba pa mdimawo.

Monga kakombo, iye amakhala pamwamba pa mdima wa matope. Iye amakhala pamwamba pa mdima wa madzi amatope. Iye amakhala mu kuwala, akuwalitsira kukongola kumene kunaikidwa mwa iye asanachoke mmatopewo. Amen.

¹¹⁰ Tsopano ine—ine ndikumverera ngati Mkristu wofuula. Chimene chinali uko ndi Mulungu, pachiyambi, chinakankha

njira yake mpaka chinadutsa, chinakagonjetsa. Icho chinagonjetsa chigoba. Icho chinagonjetsa matope. Icho chinagonjetsa madzi. Icho chinagonjetsa chirichonse, ndipo chinali m'gonjetsi, ndipo chinawalitsira kukongola ndi Ulemelero wa Mulungu.

¹¹¹ Umo ndi mmene wokhulupirira aliyense amachitira. Umo ndi mmene Nowa anachitira. Umo ndi mmene Loti anachitira. Njira yake ndi imeneyo. Taonani mnyasi zimene iye analimo. Umo ndi mmene Mose anachitira. Umo ndi mmene Yoswa anachitira. Umo ndi mmene Daniele anachitira. Umo ndi mmene Shadrecki, Misheki anachitira. Umo ndi mmene Yohane M'batizi anachitira; Zakariya, Elizabeti. Umo ndi mmene Simioni, umo ndi mmene Anna, mmodzi aliyense wa iwo anachitira. Iwo anagonjetsa matope amene anali uko powazungulira iwo ndipo anaikidwa mwa iwo. Anatukula mutu wawo pamwamba pa chinthucho, ndipo anawalitsa Ulemelero wa Mulungu. Icho ndi chimene Mkhristu weniweni amachita.

¹¹² Kumbukirani, Yesu anamusonyeza Iye mmene izo zimachitikira. Masiku forte a kuyesedwa, Iye anayesedwa kuposa munthu aliyense amene akanayesedwapo, mu mayesero a Yesu Khristu. Penyani. Iye anatisonyeza ife mmene izo zimachitidwira.

Tsopano ine nditseka, mu maminiti pang'ono chabe.

¹¹³ Taonani. Iye anatisonyeza ife mmene izo zimachitidwira. Kodi Iye anachita motani izo? Mwa Mawu. Umo ndi mmene Iye anachitira izo, pakuti Iye anali Mawu. Ndipo Yesu anati, “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga mwa inu,” inu mwabwerera ku Mawu aponso, Mawu a lonjezo. Kodi Mawu a lonjezo ndi chiyani kwa Mkhristu aliyense? “Wamkulu ali Iye amene ali mwa inu kuposa iye amene ali mu dziko.” Ndiye ine ndingagonjetse bwanji? Osati ineyo, koma Mawu amene ali mwa ine. Mawu ndi Mulungu. Zikatero ine ndigonjetsa zinthu za mdziko, chifukwa izo zikhala Mawu mwa ine. “Ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu Anga mwa inu, ndiye mungopempha zimene inu mukufuna.” Muzingopitirira kumakankha. Inu mukupita pamwamba, motsimikiza basi monga chirichonse. Mukuona? Inu mukuyenera kubwera pamwamba.

¹¹⁴ Masiku forte ake a mayesero, ndi Mawu a Mulungu Iye anagonjetsa. Ine ndikufuna kuti ndifotokeze chinachake apa kwa maminiti pang'ono. Satana anapanga ziwembu zazikulu zitatu pa Iye mu yesero limenelo. Penyani. Izo nthawizonse zimakhala mu zitatu izo. Musaiwale zimenezo. Mukuona? Iye anapanga ziwembu zazikulu zitatu, kuyambira chapamwamba mpaka chotsikitsitsa. Iye anayetsetsa mwakukhoza kwake kuti amugonjetse Iye. Koma Iye anali Mawu. Amen. Kodi Iye anagwiritsa ntchito chiyani? Iyemwini, Mawu. Kumenya kwakukulu kutatu kwa Satana kapena ziwembu pa Iye, koma

Iye anakumana nazo izo ndi Mawu. Kumenya kulikonse, Iye amakwanitsa izo ndi Mawu. Penyani izi tsopano, kuyambira cha pamwamba mpaka chotsikitsitsa.

¹¹⁵ Choyambirira chimene iye anapangirapo chiwembu chake, kuti agwiritse ntchito mphamvu Yake yaikulu. Chimene, Iye ankadziwa kuti Iye anali Mawu. Iye ankadziwa malo Ake. Inu mukukhulupirira kuti Iye ankatero? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] “Ine Mwana wa munthu.” Iye ankadziwa malo Ake. Ndipo Satana anabwera ndipo ankafuna kuti Iye agwiritse ntchito mphamvu Yake Yomwe pa Iyemwini, kuti amudyetse Iye, ankafuna kuti adzidyetse Yekha. Iye anali ndi njala. Munthu akakhala ndi njala, iye akhoza kuchita pafupifupi chirichonse. Iye amaba, amalanda, amapempha, amabwereka, chirichonse. Mukuona? Iye anali ndi nkhwiru ya kudya ija. Ndipo Satana anagwiritsa ntchito chiwembu chake choyambirira chachikulu pa Iye, kuti atenge mphamvu Yake imene Iye anali atapatsidwa kuti adzigonjetsera nayo ndikuti ayigwiritse ntchito iyo pa Iyemwini. Iye sanagwiritse ntchito iyo pa Iyemwini. Ayi. Iye ankaigwiritsa ntchito iyo pa ena. Uko nkulondola. Iye amaigwiritsa ntchito iyo pa ena, osati Iyemwini. Iyo sinali ya Iye. Ngakhale, Iye akanatha kuchita zimenezo. Iye ndithudi akanatha kuchita izo.

¹¹⁶ Koma mukuona mmene mdierekezi amachitira? Mdierekezi amafuna kuti iwe uzimusamala iye. Iye ankangosamala zokhazo zomwe Atate anati achite. Uko nkulondola.

Iye anati, “Bwanji,” Satana anati, “kwalembedwa, ‘Iye adzawapatsa Angelo mphamvu . . .’”

¹¹⁷ Iye anati, “Inde, koma kwalembedwanso . . .” Mukuona? Ndi zimenezotu. Mukuona? Iye ankadziwa Yemwe Iye anali. Satana amadziwa . . .

Lingalirolo limapita mwakuya kuposa mmene Ilo linalembedwera. Mukuona? Kudzodza kwake. Zenizeni zake ziri mkati mwa Ilo, inu mukuona, chimene Ilo liri kwenikweni.

¹¹⁸ Ngakhale Iye akanatha kuchita zimenezo, Iye sanachite izo. Koma Iye—Iye sanapereke chidwi ku maganizo a Satana.

Tsopano, apa pali chinthu chabwino. Mukuona? Nthawizina Satana akhoza kukutenga iwe, ndipo pamene iwe ukuganiza kuti iwe ukuchita chifuniro cha Mulungu, ndipo akhoza kukupangira iwe choti akambepo, iwe nkugwera izo. Inde, bwana. Iye ndithudi akhoza.

¹¹⁹ Tsopano tiyeni tingotenga, mwa chitsanzo, monga alongo athu. Iwo ndi okongola. Ndipo iye akhoza kukufikitsani inu pa malo, amene, inu mumasiya tsitsi lanu kuti likule, inu osazindikira. Ilo nkumawoneka labwino kwambiri pa inu, ndipo, chinthu choyamba inu mukudziwa, inu mumayamba kumverera modzikweza pang’ono, kukhala ngati mwapambana pang’ono chinachake. Ena a amuna inu, inu mukudziwa chimene

ine ndikutanthauza. Mukuona? Ndipo iye akhoza kutenga chinthu chomwecho ndi kukhalapo ndi chokamba pa inu. Uko nkulondola. Mwaona. Inu muyenera kugonjetsa chimenecho.

Tangokumbukirani, inu mukukhalira moyo Mulungu. Inu muli ndi cholinga chimodzi, ndipo ndicho Yesu Khristu. Kunja kwa zimenezo, kulibe chirichonse chimawerengedwa. Ameneyo ndi Iye. Kenako, chachiwiri, banja lanu. Kenako, chachitatu, inueni. Koma, choyamba, Mulungu; chotsatira, banja lanu; ndipo chotsatira, inuyo. Ndinu wachitatu; awo ndiwo mathero a ulendo. Mudziziika nokha kumapeto; Iye anatero.

¹²⁰ Taonani zimene Iye akanachita. Anati, “Ine nditha kuuza Atate Anga, akanayankhula ndi Iye, Iye pomwepo akhoza kunditumizira Ine magulu thwelofu a Angelo.” Pamene, m’modzi wa Iwo akhoza kuwononga dziko. Anati, “Ngati Ufumu Wanga ukanakhala wa dziko lino, ndiye onditsatira Anga akanamenyera. Koma Ufumu Wanga ndi wa Kumwamba.” Ndi zimenezotu. Mukuona? Iye akanatha kuchita zimenezo, koma Iye sanatero. Mukuona? Ngakhalebe, Iye akanakhoza kuchita izo. Iye sanamvetsere ku zokamba za Satana.

¹²¹ Tsopano, kodi inu mwawamvapo anthu akuti, “Ngati—ngati inu mukukhulupirira ku—kuti kuli mchiritsi Wauzimu. . . Ngati ndiwe mchiritsi Wauzimu. . . Pita ukamtenge mchiritsi Wauzimu wakoyo. Ndiri ndi munthu pano, akudwala. Ine ndikufuna ndimuwone akumuchiritsa iye.” Mukuwona mdierekezi yemwe uja? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye akuyesera kuti akambirane ndi inu. Iye akuyesetsa kukupangani inu kuti inu mumumvetsere iye m’ malo mwa Mulungu. Koma wantchito weniweni, woona wa Mulungu amamvetsera ndi kuwona chimene Atate akunena, poyamba. Mukuona?

¹²² Monga mwana wamng’ono wa a Stadskev, pamene iwo anamutumiza kuno. Ndipo Akazi a Stadskev anati, “M’bale Branham, ine ndaimba kuchokera ku Germany.” Uko kunali gulu la ankhondo la Chimereka, ndi imodzi ya ndege zawo itaima kunja uko pabwalo, ikanandiwulutsa ine kupita ku Germany ndi kubwera nane, mu tsiku limodzi. Iye anali wopempheretsa. Ndipo mwanayo anali atagona, atafa. Ndipo mayi wachichepere uyo akufuula, iye anati, “Mvetserani!” Anati, “Ine ndikudziwa. Ine ndinaima pamenepo ndipo ndinamuwona mkazi uyo atamunyamula mwana wakufayo mmikono mwake, amene anafa m’ mawa umenewo. Ine ndinamuwona M’bale Branham akuyenda akupita kumeneko, anadzaika manja pa mwana wakufayo, ndipo iye anabwerera ku moyo.” Anati, “Uyu ndi mwana wanga, M’bale Branham.” Anali asanakhalepo ndi imfa m’banja lawo. Mukuona? Ndipo kanthu kakang’ono aka kanadwala m’ mawa wina ndipo kanadzafa madzulo ake.

Apa panali onse a iwo ataima mozungulira, ndipo akupereka mauneneri ndi zinthu, “Mwanayo adzuka,” ndi zonse monga choncho.

¹²³ Ine ndinati, “Chabwino, izo nzabwino kwambiri, Mlongo Stadskev. Koma mundilole ndikawone chomwe Atate akunena.”

Ine ndinapita ku tchire. Ndipo ine ndinakapemphera. Nditabwererako; iye anali ataimba kawiri kapena katatu ine ndisanabwerere m’ mawa wotsatirawo. Kunalibe kalikonse.

A dokotala anati, “Chabwino.” Anati, “Ngati ziri zimenezo, ngati inu muli ndi chikhulupiriro chonga chimenecho, dona, ife sitimulola mwanayo kuti achoke mchipatala. Musiyeni iye agone momwe muno. Inu mukhale momwe muno ndi iye. Izo ndizabwino.”

M’bale Stadskev anapita ndipo anakamuwona wamkulu wa a nkhondo. Iwo anati, “Ndithudi. Ife timuwulutsa iye apite kumeneko, ndipo tidzamubweretsanso iye.”

¹²⁴ Ndipo apo panali ndege itaima, ikudikirira, kuti inditenge ine m’ mawa umenewo ndi kundibweretsanso usiku umenewo, wa ku Germany, ku Heidelberg, Germany, ku chiwukitsiro cha mwana uyu. Ine ndinati, “Ndithudi, Mulungu akhoza kuchita izo, koma tiyeni tiwone chimene chiri chifuniro Chake.”

¹²⁵ Kenako ine ndinachokapo, ndinakapemphera usiku wonse. Panalibe chochitika. Ndinabwereranso m’ mawa wotsatira; panalibe chochitika. Ndipo ine ndinayamba kulowa mchipindamo. Basi pomwepo ine ndinayang’ ana apo, ndipo apo panaima Kuwala kuja kutapachikika apo pa chitseko. Anati, “Usaika dzanja lako pa izo. Usadzudzule izo. Ilo ndi dzanja la Mulungu.”

¹²⁶ Ine ndinamupeza iye pa foni. Ine ndinati, “Mlongo Stadskev, kamukeni mmanda mwana wanuyo. Ilo ndi dzanja la Ambuye. Icho ndi chifuniro cha Mulungu. Chinachake chikanadzamuchitikira mwanayo panjira. Inu mumusiye iye azipita kumeneko Mulungu akudziwa kumene iye ali. Inu mukhoza kupita kwa iye tsopano. Iye ali moyo, inu simungathe. Inu mungomusiya iye chomwecho.”

¹²⁷ Mlaliki wamkulu uja wa chiLutera mu Germany analemba kalata ndipo anati, “Ine ndingayamikire chotani, chimenecho, M’bale Branham kudikirira chigamulo chomveka cha Mulungu, iye asananene chirichonse.”

Ndi zimenezotu. Muzigwira chigamulo cha Mulungu. Ziribe kanthu kuti ena akunena chiyani, kapena chirichonse chomwe icho chiri, musamakambirane ndi Satana, nkomwe.

¹²⁸ Ngati Satana akuti, “Tsopano, ubatizo wa mmadzi, dzina la ‘Atate, Mwana. . .’” Ngati izo, iye akatero, inu muzisiye izo zokha. Mulungu ananena mosiyana. Ngati iye akuti, “Inu ndi

mwamuna wabwino, inu simukusowa kutero. . . Inu ndi mkazi wabwino, inu simukusowa kuti mutero. . .” Inu musazisamale. Ngati Mawu akunena chinachake chosiyana, inu mukhale ndi Mawu mosalabadira chimene icho chiri. Ndicho chitsanzo chimene Yesu anapereka kwa inu, ndipo ndi chimenecho chiwembu chachikulu chija, mwaona, chimene iye anapanga pa Iye.

¹²⁹ Ndiye, chiwembu chachiwiri. Ine ndifulumira. Zikungowoneka ngati nthawi ikungopita mothamanga. Chiwembu chachikulu chotsatira chinali, chimene iye anapanga pa Iye, kuti Iye akhale chiwonetsero.

Ndi momwe izo zimamenyera atumiki a Mulungu, kuti akhale chiwonetsero, kuwonetsera zimene iwe ungachite. “Ulemelero kwa Mulungu! Alleluya! Ndine muwomboli! Ndine *wakuti*.” Mukuona? Mukuona?

¹³⁰ “Kwera kuno, pamwamba pa kachisi, ndipo ukhale pansi apa.” Iye anamuyesa Iye kuti achite zimenezo. Tsopano, kumbukirani, Iye anayesedwa kuti achite izo, zovuta. Anati, “Tsopano, ngati Iwe ukufuna kuti ukhale chinachake pamaso pa anthu, uyime apa pa kachisi uyu, ulumphire pansi.” Mukuona? “Ine ndikupatsa Iwe Lemba la izo, chifukwa kwalembedwa, ‘Iye adzawapatsa Angelo ulumuliro pa Iwe, kuwopetsa kuti, nthawi iliyonse, ukadzapondetisa phazi pa mwala. Iye adzakunyamulira Iwe mmwamba.’” Kumupanga Iye kukhala chiwonetsero, kuwonetsera ulumuliro Wake.

¹³¹ Palibe mtumiki woona wa Mulungu amene amachita konse zimenezo. Inu mukamuwona munthu akudziwonetsera, chidali chake panja, ndi zonse monga choncho, mudzangokumbukira, pali chinachake cholakwika pamenepo. Ayi. Mulungu samafuna zimenezo. Yesu anapereka chitsanzo. Iye akanatha kuchita izo. Iye ndithudi akanatha kuchita izo, koma Iye sanachite zimenezo. Palibe mtumiki wa Mulungu amene amakhala wodziwonetsera, yekha, kuyesera kuti atenge mphamvu za Mulungu ndi kudziwonetsera yekha pamwamba pa munthu aliyense.

¹³² Inu mukukumbukira Mose anachita zimenezo? Mukukumbukira izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Mulungu anamupatsa iye mphamvu yochita chirichonse chimene iye amafuna kuchita; anamupanga iye mneneri. Iye anayenda kupita ku Thathwe ilo, ndipo iye anakakantha Thathwelo kachiwiri. Uko kunali kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu.

Mulungu anati, “Yankhula kwa Thathwe ilo. Usalikanthe ilo kawiri. Iwe uswa zonse—zonse—choimira apa. Thathwelo ndi lakuti lidzangomenyedwa kamodzi.” Koma iye anayankhula za kufooka kwa Mawu pamene iye anachita izo; Izo sizinali zokwanira. Eya. Mawu anali chimene chimachitika. Thathwe limenelo linali Mawu. Mukuona?

133 Iye, nthawi yoyamba, iye anakantha Thathwelo ndipo madzi anatuluka. Ndipo kenako iwo anakhalanso ndi ludzu. Iye anati, “Tsopano bwerera ndipo ukalankhule kwa Thathwelo.” Ilo linangokanthidwa kamodzi. Mukuona?

“Kusakwanira kwa Mawu,” Mose anachitira umboni za izo. “Mawu sanali kulondola; Iye ankayenera kuti akanthidwense kachiwiri.”

134 Kotero Mose anapita kumeneko ndipo anakakantha Thathwelo monga choncho, anati, “Tuluka!” Sanatuluke, kotero iye analikanthanso ilo kachiwiri, ndipo anati, “Tuluka! Ine ndikukulamulira iwe kuti utuluke.” Ndipo madziwo anatuluka.

135 Mulungu anati, “Bwera kuno. Bwera kuno. Iwe wadzikuza wekha. Iwe unatenga mphamvu Zanga; m’malo mondiyetsa Ine, iwe wadziyetsa wekha. Tsopano iwe suwoloka kupita ku dzikolo. Yang’ana uko, taona mmene ilo likuwonekera; koma, apa, iwe unyamukira pomwe pano.” Oh, mai! Sipanakhalepo m’modzi wonga Mose, inu mukudziwa. Ayi, ayi.

136 Pamene iye anafika pa chiwonetsero icho ndi Yesu, iye anati, “Kwera pa kachisi apa ndipo ulumphire pansi.”

137 Iye anati, “Kwalembedwa,” ameni, “Usamuyese Ambuye Mulungu wako.” Mukuona? Iye anakumana naye iye ndi Mawu, mu zimenezo, ndi chiwembu chachikulu chirichonse.

138 Palibe mtumiki woota amayesera kudziwonetsera yekha, ndi—ndi mphamvu ya Mulungu. Iye akatero, iye amagonja pomwepo.

139 Chiwembu chachitatu chachikulu, Satana anadzipereka kuti alanditsa ufumu uno kwa Iye. Iye anatero. Satana anati, “Mukuwona maufumu awa a mdziko? Awa ndi anga. Ine ndimachita nawo iwo chirichonse chimene ine ndingafune. Ine ndiwalanditsa iwo kwa Inu.”

Koma, inu mukukumbukira, iye anali kuyesera kuti amupangitse Iye kuti alilanditse mopanda mtanda. Ngati Iye akanatero, ife bwenzi titataika. Iye akanatha kuwutenga ufumuwo. Koma Iye ayenera kutsatira chi...Iye ayenera kubwerera. Iye anayesedwa kuti achite zimenezo, tsopano. Imfa ndi chinthu chovuta. Iye anayesedwa kuti atenge ufulu Wake ndi kudzakhala Mfumu ya pa dziko lapansi, mopanda mtanda. Koma, ngati Iye akanatero, anthu Ake akanafa. Satana mokondwera akanakamba zimenezo kwa Iye. Koma Iye anati, “Pita kumbuyo Kwanga, Satana.” Iye sanachite izo.

140 Iye anabwera ndipo anadzavutika, ndipo anadzatenga njira yolimba, yovuta. Iye anadzatenga njira ya mazunzo. Iye anadzatenga njira ya imfa.

Kodi ife, m’mawa uno, tikulolera kuti titero, titenge njira yomweyo imene iye Anatenga? Kodi ndife lolera kuti tife? Kodi

ndife ololera kuti tidzipereke tokha kwa Mulungu, kulanditsa dziko lonse ndi zinthu, kuti tikamutumikire Iye? Mukuona?

¹⁴¹ Tsopano, Iye analephera kuti achite izo. Analolera ku—kuti alilanditse ilo, Satana anatero, kwa Iye. Koma Iye sanachite izo. Ngakhale Yesu anayesedwa, Iye anatigonjetsera ife. Iye—Iye anapirira mayesero onse chifukwa cha ine ndi inu. Mukuona? Iye akanatha kulitenga ilo pomwepo. Koma Iye anatengeranji njira inayo? Kuti ife tidzathe kubwera, ndi kudzakhala ndi Iye. Ndipo ngati Iye anapereka mtengo uwo ngati umenewo, ndiye ife tingakhale ochepa bwanji kuti tibatenge izo? Pamene, kumbukirani, kulibeko chirichonse kuno, mulimonse.

¹⁴² Ngati inu mutakhala zaka handiredi, kodi inu mungadzakhale chiyani? Wamisala, ndipo malingaliro anu kusongonekera, zonse kulumala, ndi wokalamba ndi wamanjenje. Ndiko kumene inu mukupita, ndipo ndiwo mathero a izo. Inu mubwere tsopano, mugonjetse chinthucho. Inu muchita motani izo? Mwa Mawu. Chimene Mawu anena, inu mukachite chimenecho. Muzikayenda modzichepetsa. Muzikakhala moyo motsatira Yesu.

¹⁴³ Iye anapirira zinthu zonse chifukwa cha inu ndi ine. Iye ndi chitsanzo chathu momwe tingagonjetsere m'badwo wathu woipa, monga Iye anagonjetsera m'badwo Wake woyipa.

¹⁴⁴ Kumbukirani, pamene Iye anadzabwera pa dziko lapansi, kunalinsu kusakhulupirira kochuluka chimodzimidzi basi, kapena kochulukirapo, kuposa mmene zinayamba zakhalirapo pa nthawi iliyonse. Izo sizinamusokoneze Iye mpang'ono pomwe. Pamene iwo anamutcha Iye mdierekezi m'malo mwa Mulungu, pamene iwo anamutcha Iye chirichonse chimene chikanachitidwa, izo sizinamusokoneze Iye mpang'ono pomwe. Iye anali ndi cholinga chimodzi: “Kusamala Atate. Kusunga Mawu.” Mawu ndi Mulungu. Iye anali mtima umodzi.

¹⁴⁵ Ife nthawizina timayesedwa kuti tibwerere mmbuyo. Ambiri a inu, mwayesedwapo kuti mubwerere ku chipembedzo, kubwerera ndi kukatenga, chifukwa dziko lonse likuti, “Ndinu a chipembedzo chiti? Ndinu a mpingo wanji?” Ife timayesedwa kuti tichite zimenezo; tonse a ife. Alongo athu amayesedwa kuti abwerere mmbuyo, abwerere ndi kukajowinana ndi mipingo inayo, ndi ena a Assemblies, kapena mipingo ya Mulungu, kapena ina ya iyo; kukhalabe a Pentekoste, kumalola tsitsi lanu kuti lizidulidwa, ndi kumavala basi mulimonse mmene inu mukufunira. Mukuona? Inu mumayesedwa kuti muchite zimenezo, kubwerera ndi kukhala wotchuka ndi m'badwo woyipa uwu umene ife tikukhala nawo.

Pamene, ili ndi tchimo lalikululu la masiku athu. Ilo ndi tchimo lalikululu pakati pa anthu athu, chidziko, monga Baibulo linanenera Laodi-. . . M'badwo wa Laodikaya unali. Iwo ndi wa chidziko, “Wolemera, sakusowa kanthu; sakudziwa kuti iye

ndi wa maliseche, womvetsa chisoni, wausiwa, ndi wakhungu.” Ndiro tchimo la tsiku lathu. Pamene inu mumva Mawu a Mulungu akuitana motsutsa izo, ndiye inu mumatenga njira inayo, ndinu osatchuka ndi dziko. Inu mumayesedwa kuti mubwerere mmbuyo.

¹⁴⁶ Ine ndikudziwa. Inu mumakhala mukunena ndi ine. Ine ndikudziwa inu mumalankhula, “Nthawi zonse.” Ine ndikudziwa inu mumatopa nane ine ndikamaimba zeze pa zinthu izi. Ine zimanditopetsa kukuwonani inu mukuchita zimenezo, inenso, uko nkulondola, tchimo ili limene ine ndikuyesera kuti ndikuuzeni inu. Mukuti, “Kodi inu mukuimbiranji zeze pa ilo?” Musiye kuchita zimenezo, ndiye. Ine ndikuyesetsa kuti ndipulumutse moyo wanu, ndi Mawu. Ine zimanditopetsa, nanenso. Chotero, mungowongoka. Ili ndi tchimo, silikuyenera kuti lizichitidwa. Inde, bwana.

¹⁴⁷ Ife ndi akuti tizigonjetsa zinthu izi. Ife timayembekeza kuti tiziyesedwa ndi izo, dziko. “Inu mukakonda dziko, zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu,” anatero Yesu.

¹⁴⁸ Tsopano ife tingotseka, ponena izi. Pali mphotho ya kwa ogonjetsa.

¹⁴⁹ Mundilole ine ndiwerenge chinachake apa kwa inu. Mutsegule mu ma Baibulo anu. Tiyeni tibwerere ku Chivumbulutso, mutu wa 3, wa 2. Penyani apa tsopano, zinthu zonse izi ine ndakhala ndikukamba za, kugonjetsa. Tsopano tangodziyang’anani nokha ndipo muwone. Mudzifufuze nokha mu kalilole wauzimu, muwone ngati inu mwagonjetsa.

¹⁵⁰ Tsopano, uthenga woyamba, kwa—kwa m’ngelo wa Efeso, ine ndikufuna kuti inu mumvetsere kwa zimene Iye ananena. Ndipo Chivumbulutso, mutu wa 2, ndime ya 7. Izi ndi za kwa m’badwo wa mpingo umenewo, pamene Iye anawauza iwo zonse zomwe iwo anachita, “Anasiya chikondi chawo choyamba.” Ndime ya 7:

Iye amene ali ndi khutu, msiyeni iye amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo; Kwa iye (munthu, osati mpingo) . . . Kwa iye amene agonjetsa—agonjetsa Ine ndidzampatsa kuti adye za mtengo wa moyo, umene uli pakati pa paradiso wa Mulungu.

Mukuona? Agonjetsi mu Efeso.

¹⁵¹ Tsopano, wotsatira unali Simurna. Tsopano, kwa ogonjetsa mmenemo, ife tikumvetsera kwa izi. Tsopano, ndime ya 11.

Kwa iye—iye amene ali ndi khutu, msiyeni iye amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo; Iye amene agonjetsa sadzapwetekedwa ndi imfa yachiwiri.

Mukuona? Iwo anagonjetsa izo.

¹⁵² Tsopano, izo, tsopano muyang'ane ku Pergamo, ife tipeza chimene mgonjetsi anamusiyira iye, mu umenewu. Ife tiwerenga ndime ya 17, kwa mpingo wa Pergamo.

Iye amene ali ndi khutu, . . .

Uyo, uyo ndi munthu payekha, osati gulu lonselo. Munthu payekha, ameneyo ndi Mkwatibwi akutuluka, inu mukuona, Mpingo.

Msiyeni iye amene ali ndi khutu, amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo; Kwa iye amene agonjetsa Ine ndidzampatsa kuti adye manna obisika, ndipo ndidzampatsa iye mwala woyera, ndipo mmwalamo dzina latsopano litalembedwa, limene palibe munthu akulidziwa kusungira iye amene alandira izo.

Izo ndi za kwa m'gonjetsi, wa m'badwo wa mpingo.

¹⁵³ Tsopano, wotsatira ndi wa Tiyatira. Tiyeni tipeze chimene mgonjetsi anali nacho mu tsiku limenelo. Tiyeni titenge ndime ya 26.

Ndipo iye amene agonjetsa, ndi kusunga ntchito zanga mpaka kumapeto, kwa iye ine ndidzampatsa mphamvu pa mafuko: (Uko nkulondola.)

Ndipo . . . adzawalamulira iwo ndi ndodo ya chitsulo; ndi monga chiwiya cha owumba iwo adzasweka mu zidutswa: ngakhale monga ine ndinalandira za Atate anga.

Mwaona, “Ali ndi Iye, mu mpando Wake.” Khristu ndi wakuti adzalamulira mafuko, ndi ndodo ya chitsulo. Ndipo apa pali Mpingo umene wagonjetsa, “Utakhala mmenemo, limodzi ndi Iye, kuti akaswe mafuko ndi ndodo ya chitsulo.”

¹⁵⁴ Tsopano tiyeni tiwatengere iwo ku Mpingo wa Sarde. Tsopano ndime ya 5 ya mutu wa 3.

Iye amene agonjetsa, omwewo adzavekedwa chovala choyera; ndipo ine sindidzafufuta dzina lake mu bukhu la moyo, koma ine ndidzatchula dzina lake pamaso pa Atate anga, ndi angelo oyera.

Izo ndi za kwa ogonjetsa mu Sarde.

¹⁵⁵ Tsopano, tiyeni titenge tsopano ndime ya 12. Tsopano, izi ndi za kwa mpingo wa—wa Filadefiya, mu ndime ya 12.

Iye amene agonjetsa Ine ndidzampanga mzati mu kachisi wa Mulungu wanga, ndipo iye sadzapitanso panja: ndipo Ine ndidzalemba pa iye dzina langa, dzina la Mulungu wanga, ndi dzina la mzinda wa Mulungu wanga, umene uli Yerusalemu watsopano, umene ukutsika kuchokera kumwamba kuchokera . . . Mulungu: ndipo ine ndidzalemba pa iye dzina langa latsopano.

156 Penyani chimene mgonjetsi akulonjezedwa. Mukuona?

Tsopano, tsopano Laodikaya, uwo ndi m'badwo wa mpingo wotsiriza. Mukhala ogonjetsa ena mmenemo. Penyani apa. Iwo, kumbukirani, m'badwo wa mpingo uliwonse, umene ukutsogolera iwo umatenga zonse zimene inayo inapereka. Penyani pamwamba apa. Tsopano, apa, izo zinali atatha kulandira mphamvu zonse izi, maina atsopano awa, ndi chirichonse cholembedwa, chimene Iye analonjeza, ndi kudya manna obisika, ndi kudutsa monse. Penyani m'badwo wotsiriza uwu, Chivumbulutso 3:21.

Kwa iye amene agonjetsa ine ndidzamulola kukhala ndi ine mu mpando wanga, (ameni), ngakhalenso monga ine ndinagonjetsa, ndipo ndikukhala pansu ndi Atate anga mu mpando wake.

Iye amene ali ndi khutu, msiyeni iye amve chimene Mzimu ukunena kwa mipingo.

157 Pali mphotho kwa ogonjetsa. Limbikirani, kakombo. Ngati izo ziri mwa inu, musiye pambali matope ndi china chirichonse, ndipo mukunikizire pamwamba. Inde, bwana. “Kuti mudzakhale ndi Ine pa mpando Wanga.”

158 Inu mukudziwa, nthawi ina, amake a Yakobo ndi Yohane . . . Ife sitikhala ndi nthawi kuti tiwerenge izo. Amake a Yakobo ndi Yohane anabwera ndi kudzapempha malo awa. Inu mukudziwa zimenezo? Mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] “Ambuye, mumulole mwana wanga akhale kumbali imodzi, ndi mwana wanga winayo akhale kwinko.” Ndi chimenecho chokhumba cha mayi kwa mwana wake.

Koma penyani. Koma, “Malo amenewo,” Yesu anati, “anakonzedweratu.” Malo awa panalibepo pa nthawi imeneyo. Bwanji? Zindikirani. “Iwo adzaperekedwa kwa iwo amene anawakonzera.” Chiyani? Amene ali oti adzakakhale pa dzanja lamanja, ndi ena apafupi zedi ndi Iye, anali woti adzakhala wogonjetsa. Mukuona? Izo zinali apobe . . . Iye anati, “Ine—ine sindipereka izi. Ine sindingapereke izi, koma izo zidzaperekedwa pambuyo pa mayesero.” Ameni. Mukuona? “Ine sindingathe kupereka izi. Koma mayesero akadzabwera, iwo adzakakhala kudzanja lamanja ndi la kumanzere. Ndi imeneyo mbewu yokonzedweratu ikudikirira zimenezo kutsidya uko. Izo zidzaperekedwa kwa iwo amene izo zinalonjezedwera. Izo zidzakaperekedwa kumeneko, koma yesero silinabwere apabe; limenelo, iye sanagonjetsebe.” Mukuona?

159 Munthu amene anali woti adzatenge malo awa kumbali imodzi, ndi wina kudzatenga kumbali inayo, moyandikana ndi Iye mu Ufumu, iwo anali asanaperekedwebe, mwaona, anali asanagonjetse. Yesero linali lisanagwebe. “Ilo lidzagwa mtsogolo.”

“Ngati ife tivutika chifukwa cha Khristu ndi Mawu Ake, ife tidzalamulira limodzi ndi Iye, pakuti Iye ndi Mawu.” Kumbukirani, “Ngati ife tivutika chifukwa cha Iye ndi Mawu Ake, ife tidzalamulira limodzi ndi Iye, mu Mawu Ake.”

¹⁶⁰ Zindikirani. Iye, Chitsanzo chathu, anagonjetsa, ndipo atatero anakwera mmwamba, Iye atatha kugonjetsa imfa, gehena, matenda, manda. Chirichonse, Iye anagonjetsa. “Atatero Iye anakwera mmwamba, ndipo anatsogolera amsinga ukapolo, anapereka mphatso kwa anthu.” Icho chinali Chipangano Chakale, ndi overa a Chipangano Chakale amene anali atagonjetsa. Iwo ankafunafuna Munthu woteroyo, ndipo iwo anafa Iye asanafike kumeneko. Koma pamene Munthu yu anabwera, “Izo sizinawalepheretse iwo amene anali akugona.” Ameni. Sangalephere, mulimonse. Kukhala moyo kapena kufa, kodi zimapanga kusiyana kotani? “Sizidzawalepheretsa.” Mukuona? Iwo ankafunafuna chimenecho.

¹⁶¹ Ngakhale Yobu kumbuyo uko, iye ankafunafuna chimenecho. Iye anati, “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi.” Ndi ameneyo munthu wolungama, munthu wangwiro. Iye ankapereka nsembe. Iye amachita chirichonse chimene Mulungu anamuza iye kuti achite. Iye ankachita izo ndi ulemu ndi kulemekeza. Iye anali mneneri. Ndipo zitatero Satana anabwerapo, kuti adzamuyese iye. (Chimodzimodzi monga iye amabwera kudzakuyesani inu.) Kodi iye anachita chiyani? Iye anakhala akuimabe kumeneko.

Ngakhale mkazi wake anatulukira, ndikuti, “Kodi simumutukwana Mulungu ndi kufa imfa? Iwe ukuwoneka womvetsa chisoni kwambiri utakhala pamenepo.”

¹⁶² Iye anati, “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa.” Tsopano, iye sananene kuti iye anali wopusa, koma amayankhula ngati ameneyo. Mukuona? Anati, “Iwe ukuyankhula ngati mkazi wopusa.” Anati, “Ambuye anapereka, ndipo Ambuye alanda; lidalitsike Dzina la Ambuye.” Iye anagonjetsa.

¹⁶³ Iye anagonjetsa zimene oyandikana nawo ankanena. Iye anagonjetsa zomwe mamembala onse a mpingo, Bilidadi ndi onse, ankanena. Iye anagonjetsa bishopu ndi zimene iye ankanena. Iye anagonjetsa akardinolo ndi zimene iwo ankanena. Iye anagonjetsa chipembedzo, zimene iwo ankanena. Ndipo iye anakhala ndi kulungamitsidwa kwa Mawu. Ameni. Komabe, izo zinamutengera iye chirichonse chimene iye anali nacho, ngakhale ana ake. Iye amakhula zilonda ndi phale, atakhala pamenepo, ndipo komabe iye anagonjetsa. Ndipo pamene ora lalikulu la mayesero potsiriza linapambana, ndiye mitambo inapiringizira mmbuyo.

¹⁶⁴ Iye anayang’ana pa chinthu chanzeru chirichonse. Iye anati, “Pamakhala chiyembekezo pa mtengo ngati iwo ufa; iwo

umadzakhalanso moyo. Ndipo mbewu ikagwera mnthaka, iyo imavunda; iyo imadzakhalanso moyo. Koma munthu akagona panso ndipo napereka mzimu; iye amavunda. Ndipo ana ake amabwera, ana ake aamuna, kudzalemekeza ndi kudzamulira iye; iye samazindikira izo ayi. Iye samaukanso. Oh, ndi zimenezotu. Vuto ndi chiyani? Ndine mbewu, nanenso. Ndine chinachake, chimene chiri mbewu, ndipo ine ndidzapita ku nthaka. Ine sindidzawukanso. Ine ndidzakagona mmenemo. Oh, ndibiseni ine mmanda, ndisungeni ine mmalo achinsinsi mpaka mkwiyo Wanu utadutsa. Ndisankhireni ine nthawi ndipo dzandiweruzeni ine. Pamene miyala inyenyeke, madzi anyenya miyala.” Oh, iye anapitirira, akunena zinthu zonse izi. Iye amatha kuwona zitsanzo zonse kunja uko, chimene izo zinali. Oh, iye samatha basi kuziwona izo.

¹⁶⁵ Ndipo, Mlongo Rodgers, mukukumbukira pamene ine ndinalalikira izo pa maliro a Busty. Mukuona?

¹⁶⁶ Mmene, izo, “Iye amatha kunyenya mwala,” mmene zinthu izi. “Oh, O Inu, ndibiseni ine mmanda, ndipo mundisunge ine mmalo obisika.” Iye anakhala akulimbikirabe. Iye anati, “Ine ndikanakonda ine ndikanadziwa. Ine ndikanakonda ine ndikanadziwa kumene ine ndingapite, kwa Munthu amene angaike manja Ake pa ine, munthu wochimwa, ndi pa Mulungu woyera, ndi kundiyankhulira ine kwa Iye.” Oh, mai! “Iye Alipo. Ine ndikudziwa Iye Alipo. Pali Winawake Apo amene angathe kuchita izo. Pali Winawake penapake. Ine ndingakampeze kuti Munthu ameneyo? Ndingakampeze kuti? Ine ndikagogoda pa khomo Lake ndipo ndikayankhula naye Iye. Ngati Winawake atangoika dzanja Lake pa ine, ndi pa Mulungu, ndi—ndi kundikonzera ine njira, kundiyankhulira! Ngati ine nditangompeza Munthu ameneyo! Oh, kodi Iye ali kuti?”

¹⁶⁷ Iye anafufuza kudutsa mpingo wake. Iye anali atafufuza kudutsa bungwe lake. Iye sanathe kumupeza Munthu woteroyo.

¹⁶⁸ Ndipo zonse mwakamodzi, mitambo inapiringizira mmbuyo, ndipo iye anamuwona Munthu ameneyo akubwera. Oh! Mtima Wake wokalamba unagunda ndi chisangalalo. Kenako chinachake chinachitika. “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo. Alipo Munthu woteroyo.” Ameni. Akadalipobe Munthu woteroyo. “Ine ndikudziwa Muomboli wanga ali moyo. Ndipo ngakhale, mphutsi za pa khungu zitadya thupi ili, komabe mthupi langa ine ndidzamuwona Mulungu, Amene ine ndidzamuwona ndekha. Iye adzaima pa dziko lapansi pa tsiku lotsiriza.”

¹⁶⁹ Mmawa wa Isitara uja, pamene Iye anawuka kutali uko, ndipo thupi la Yobu litangokhala osati kuposera phulusa la nsupuni, iye anali akudikirira. Iye anali Gulu losankhidwa lija. Iye anauka mmanda ndipo anadzalowa mu mzinda, limodzi ndi

Abrahamu, Isaki, Yakobo, Yobu. Oh, mai! Ameni. Pakuti, iwo ankamfunafuna Munthu woteroyo.

¹⁷⁰ “Ndipo kwa iwo Amene akuyembekezera Khristu nthawi yachiwiri,” amene akhoza kugonjetsa zinthu za mdziko lino, mwa chisomo Chake, kubwera mwa Iye, ndi kutseka maso anu kwa chirichonse koma Iye ndi Mawu Ake, “Iye adzawonekera nthawi yachiwiri mu Ulemelero.”

“Pakuti lipenga la Mulungu lidzawomba, akufa mwa Khristu adzauka; iwo amene ali moyo ndipo atsalira adzasinthidwa, mkamphindi, nkuthwanima kwa diso, adzakwatulidwira mmwamba limodzi, kukakumana naye Iye mu mlengalenga.”

¹⁷¹ Kaya ndidzakhala ndiri phulusa lodzadza nsupuni, kapena ine ndidzakhala ndiri moyo pamene Iye azidzabwera, izo sizikundichitira ine kusiyana kulikonse. Ameni. Ziribe kanthu, chifukwa ine ndagwira masomphenya. Chophimba chapiringizidwira mmbuyo, ndipo ine ndikumuwona Iye. Mmodzi amene atha kuima, ndi kudzaika dzanja Lake pa ine, munthu wochimwa, ndi pa Mulungu woyera. Ndipo Iye ndi chitetezero changa. Iye ndi Mawu amene ine ndimawaimirira. “Pachiyambi panali Mawu.” Iye ndi Mawu amenewo, ndipo Iye amandiimirira ine, Pamenepo. Ameni. Ndipo ine ndidzafuula izo, bola ngati ine ndidzakhale ndi mpweya, “Iye ndi Chiukitsiro changa ndi Moyo wanga.” Ndipo maziko ena onse ndi mchenga wotitimira. Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

¹⁷² Monga Iye anawatenga iwo amene ankafunafuna icho, chomwechonso Iye adzabwera kwa woyera aliyense wa Chipangano Chatsopano amene wagonjetsa kutsutsa kulikonse kwa chipembedzo, amene wagonjetsa machimo otchuka onse a tsiku lino, a m’badwo uno umene ife tiri nkukhalamo tsopano, monga Iye anachitira mmibadwo ya mpingo ina yonse, iwo amene amagonjetsa mu m’badwo wa mpingo umenewo. Iwo amene amagonjetsa chiyani? “Ndine wolemera. Ine sindisowa kanthu. Ine ndiri. . . Oh, ndine zonse *izi* ndi zonse *izi*. Ndipo ndine Mkwatibwi. Ndine *ichi*. Ine sindikusowa kanthu.’ Ndipo osadziwa kuti ndiwe wamaliseche, wakhungu.”

¹⁷³ Mwawuwona m’badwo wachinyengo uja umene ine ndimaunena? Izo sizikufanana ndi iwo amene anadulidwa mitu yawo, kumbuyo uko, kuti apeze mwala woyera; osati iwo amene anafa mu kufera, ndi kuwotchedwa pa nkhu, ndi zinthu monga izo; amene anapeza korona. Koma ndi m’badwo wachinyengo uwo tsopano, umene amaganiza kuti iwo ali chirichonse. “Chabwino, ndine membala wa mpingo. Ndine munthu wabwino. Ndine mkazi wabwino. Ine ndimachita *ichi*. Ine sindisowa kuti ndizichita *Ichi*.”

¹⁷⁴ “Koma iye amene agonjetsa,” iye amene agonjetsa zinthu za mdziko zonse izo za m’badwo uno, kodi iwo adzachita

chiyani? Onse adzakakhala ndi Iye mu mpando Wake; adzapita mu Mkwatulo pamene Iye adzabwera. Oh, mai! Kodi ine ndisamale chiyani, ndiye? Tidzizamala chimene dziko likunena? Tidzizamala chimene aliyense akunena? Mzimu Woyera waukulu uli pakati pathu. Lawi la Moto Lake likutitsogolera ife ndi kutilondolera ife. Mawu Ake atsimikiziridwa pakati pathu. Chikondi Chake chiri mu mtima mwathu. Dziko liri mmbuyo. Ife tadutsa kuchoka ku imfa tapita ku Moyo. Dziko limaganiza kuti ndinu amisala.

Koma kodi Yesu anyamule mtanda uwu yekha,
Ndipo dziko lonse lipite mwaufulu?
Pali mtanda wa aliyense,
Ndipo pali mtanda wa ine.

¹⁷⁵ Zaka sate-firii mu utumiki, ndipo mtanda wopatulika uwu ine ndidzaunyamula mpaka imfa idzandimasule.

¹⁷⁶ Ndikhoza kulolera abale anga andikane ine, anene chirichonse chimene iwo akufuna kunena, chimene akundikanira ine. Koma pa Mawu *awa* ine ndaima, ndipo Awa okha.

Mtanda wopatulika uwu ndidzaunyamula
Mpaka imfa idzandimasule ine,
Ndipo kenako ndidzapita Kwathu, mu
Mkwatulo, kukavala korona.

¹⁷⁷ Ndizo zimene ife tonse tikufuna. Si choncho? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndizo zimene ife tikufuna. Ndicho chathu—ndicho chiyembekezo chathu ndi chopempha. Ife tiribe malingaliro ena, koma chimodzi icho pa Yesu Khristu. Ndipo pa chirungamo Chake ife taima, tokha, ndi chirungamo Chake mu Mawu Ake. “Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” Ndipo Mawu akudzitsimikizirabe Okha.

¹⁷⁸ Kugonjetsa motani? Potenga Mawu, lonjezo, modzichepetsa, kuyenda modzichepetsa.

Mtanda wopatulika uwu ndidzaunyamula
Mpaka imfa idzandimasule,
Kenako ndidzapita Kwathu, kukavala korona.

¹⁷⁹ Pakuti, “Pamene Lipenga ilo lidzidzawomba!” Inu mukhoza kundiika ine mnyanja, koma Lipenga lidzandidzutsa ine. Kulondola. Ine ndidzapita Kwathu, tsiku lina. Ameni. Kufikira nthawi imeneyo, ine ndidzivutikabe, ameni, ndikunyamula mtanda uwu; nditaika maso anga osati pa anthu, koma pa Gologota kutali, pakuti Iye anali chitsanzo changa. Iye anandisonyeza mmene ndingachitire izo. Ndipo chitsanzo Chake, ife mokondwera tidzachitsatira icho, tsiku ndi tsiku.

Ndimtsatira Yesu phazi ndi phazi.
Ndimtsatira Yesu phazi ndi phazi.

180 Kodi inu simumaikonda iyo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Oh, mmene ine ndikuganizira, kumutsatira Iye, tsiku ndi tsiku, phazi ndi phazi.

Tiyeni ife tipemphere.

181 Ambuye Yesu, ora ndi maminiti fifitini tsopano, nditaima pano, kuyesera kuti nditenge Mawu Anu ndi kuwafotokoza kwa anthu mmene angagonjetsere. Inu munatiuza ife mmene izo zimachitidwira. Inu simunangotiuza ife, koma Inu munatiwonetsa mmene izo zinachitidwira. Inu munatitsogolera ife. Inu munatisonyeza ife mmene tingachitire izo: kulandira Mawu mkati mwa ife, ndi kukhala otsimikiza kuti tikugwira ku Mawu amenewo, “Kwalembedwa,” mu yesero lirilonse; koma kukhala odzichepetsa, kuyenda modzichepetsa. Zikatero ndiye kuti tagonjetsa, kudzera mwa Inu, kudzera mu mphamvu Yanu imene inamgonjetsa kale mdani wathu. Ndipo chinthu chokha chimene ife tiyenera kuchita ndi—ndi kungoyenda modzichepetsa ndi chikhulupiriro, tikukhulupirira Zimenezo, ndi batchi yathu ya kudzindikiritsidwa ya Mzimu Woyera, ndipo Satana ayenera asunthepo.

182 Pali mipango ili apa. Iyo ikuimira anthu odwala. Iwo ndi osowa, Ambuye. Ndipo iwo amawerenga mu Mawu osalephera awa pamene iwo anatenga kuchokera pa thupi la Paulo Woyera mipango ndi zovala. Izo zinakaikidwa pa anthu odwala. Mizimu yoipa inatuluka mwa iwo, ndipo zozizwitsa zazikulu zinachitika. Tsopano, Ndinu Ambuye Yesu yemweyo lero.

183 Paulo analalikira Mawu awa, ndipo analemba Mawu awa, Mawu omwewa amene ife tikuyesera kuti tiwatsatire. Chifukwa, iye anatenga Chipangano Chakale ndipo anachifanidzitsa icho, ndi kuwonetsa kuti icho chinali choimira, kuti Chipangano Chakale chonse chinali choimira changwiwo cha Chatsopano. O Ambuye, mutilole ife titsatire chitsanzo chimenecho.

184 Ife tikuwona Ambuye athu, zimene Iye anachita. Ndipo ife tikuzindikira zimenezo, oyer a Chipangano Chakale aja, mmawa uno, ife tikupeza kuti iwo anapita. Pamene Yesu anauka, iwo anapita naye Iye. Ndipo, Ambuye, ife tikukhulupirira kuti ife tidzapita pamene Iye adzawomba Lipenga. Ife tikukhulupirira izo, kuti Mkwatibwi adzapita pa Tsiku limenelo ndipo adzakalumikizana ndi—ndi gulu la Ahebri la Iwo, ndipo, limodzi, padzakhala Phwando la Chikwati mu Ulemelero. Iwo akudikirira.

Ife tikupemphera tsopano chifundo Chanu ndi chisomo pa ife. Agonjetsi, Ambuye, agonjetsi, ife tikukhumba titakhala. Tigonjetseni ife. Ambuye Yesu, Inu munaligonjetsa dziko. Tsopano ine ndikupemphera kuti Inu mumulole munthu aliyense pano, mmawa uno, “Ayike tchimo lirilonse kumbali, ayike kumbali cholemtsa chimene sichimachedwa kutifooketsa ife,

kuti ife tikathe kuthamanga ndi chipiriro liwiro limene laikidwa patsogolo pathu.”

¹⁸⁵ Paulo anayankhula izi, Atate athu Akumwamba, uko mu Bukhu la Ahebri, kuti, “Ife tiyike kumbali cholemetsa chirichonse,” mutu wa 12 uwo, umene iye anayankhula izi, iye atha kale kuwonetsa mwachitsanzo, kumbuyo uko: iwo amene anapita chitsogolo; iwo amene sanapite chitsogolo; iwo amene mofunda anatsatira; iwo amene anatsatira kutsogolo; iwo amene anatsalira mmbuyo. Onse, Iye anasonyeza zitsanzo. Kenako iye anapotoloka ndipo anati, “Tiyeni tiyike kumbali cholemetsa chirichonse, chinthu chaching’ono chirichonse chimene chimatifooketsa ife, kuti ife tikathe kuthamanga ndi chipiriro liwiro limene laikidwa patsogolo pathu; tikuyang’ana kwa Iye, woyambitsa ndi womalizitsa wa Chikhulupiliro chathu, Amene anati patse ife chitsanzo.” Ife tikuchita izo mmawa uno, Atate.

¹⁸⁶ Tsopano, ndi mitu yathu yoweramitsidwa, tsopano mufufuze mosamalitsa kwenikweni, kwenikweni, mosamalitsa kwenikweni. Ndipo, ndiye, mukhale owona mtima mwakuya kwenikweni. Izo basi—izo zimangotengera...Ndizo zonse zomwe zimatengera: kudzifufuza kwanu ndi kuwona mtima kwanu. Mukhale osamalitsa kwenikweni pamene inu mukudzifufuza tsopano. “Ndifufuzeni ine, Ambuye. Mundiyeze ine. Kodi muli choipa mwa ine? Ngati chiripo, Ambuye, mundilole ine ndichisiye icho pansu, pomwe pano tsopano. Malo ano, pomwe ine ndawelama, ndi pa guwa Lanu. Ine ndikuchiika pansu icho, pompano tsopano, ndikuikapo phazi langa pa icho. Pamene ine ndizichoka, icho chikhala chiri pamene. Mphamvu ya Magazi Anu inyeketsa icho. Ine ndikufuna kuti ndikhale m’gonjetsi. Ine ndiri ndi chinachake chimene chikundivutitsa ine, Ambuye. Ine ndikufuna kuti ndigonjetse, m’mawa uno. Ine ndikhoza, mwa Inu. Ine ndinauzidwa zimenezo, ndi Mawu Anu. Ine ndikuchiika icho pansu tsopano, Ambuye, ndipo ine ndikuika phazi langa pa icho. Pamene ine ndizituluka mnyumba ino mmawa uno, kupita, ndikudziwa kuti icho chaikidwa mu—mu msambidwe wa cholekanitsa cha Mulungu. Icho sichidzakumbukiridwanso. Ine tsopano ndikuvomereza izo ndipo ndikupempha chifundo.”

¹⁸⁷ Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, maso athu titatseka; mitima yathu tikuganizira, ndiro khomo la ku moyo tsopano. Kodi pali chinachake chimene inu mukufuna kuti muchiike kumbali mmawa uno, chinachake chimene inu mukufuna kuti mugonjetse? Ndipo inu mwayesera icho molimba kwambiri, koma, mmawa uno, inu mungosiya kumayesera. Inu mungovomereza zimene Iye anachita. Ine ndikufuna inu mungokweza dzanja lanu, ndikuti, “Ambuye, ine ndikufuna ndigonjetse. Chinthu chinachake chimandivutitsa ine.”

¹⁸⁸ Ambuye Yesu, Inu mukuona manja amenewo. Tsopano, ngati wantchito Wanu, ndaima pakati pa amoyo ndi akufa, ine ndikudzudzula chirichonse chimene chikuwawutitsa anthu awa ndi inemwini. Ndipo ine ndikupempha izo mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikhoza kuzisiya izo zitakhala apa pa guwa la Mulungu, ndi kuchokapo mmawa uno, amfulu, ngati agonjetsi.

¹⁸⁹ Ngati alongo athu sanakhalepo ndi chisomo m'mbuyomu, mulole icho chiperekedwe tsopano, Ambuye. Ngati abale athu sanakhalepo ndi chisomo, mulole icho chiperekedwe tsopano. Ndipo mulole, modzichepetsa, mayi ndi ana ake, mmalo mokhala amwano. Iye akudziwa iye akukhala. . . Iye ndi mlaliki kwa ana aang'ono awo. Moyo wake ndi chitsanzo. Abambo ndi chitsanzo kwa amayi, pakuti iye ndi mutu wa nyumbayo. Amayi akhala akuyesetsa kuwalamulira iwo; iye sakachitanso izo panonso. Ngati iwo akhala akumugwiritsa ntchito iye ngati chopondera pansu, izo sizikachitikanso. Iye ndi wothandizira. Perekani izo, Ambuye. Mulole zinthu zonse izi zimene zimatitchinga ife, Ambuye, zichotsedwepo.

¹⁹⁰ Ife—ife tikudzipereka tokha, Atate, chifukwa cha nthawi ya moyo imene ife tiri nayo patsogolo pathu, tikudziwa ichi, kuti ife tidzayenera kudzafika kumapeto a izi, ndipo izo pomwepo. Kotero, mmawa uno, ife tikutenga mwayi uwu, utatha Uthenga uwu. Ife tikutenga mwayiwu, Ambuye, kuti tibwere, chifukwa ife tapemphedwa kuti tibwere. “Ikani nkhwana zanu pa Iye, pakuti Iye amakusamalirani inu.” Ine ndikudziwa Inu mumasamala, Ambuye. Inu munasamala mokwanira potifera ife. Ndipo ife ndithudi tikhoza kusamala mokwanira pobwera ndi kudzavomereza chimene Inu munachifera.

¹⁹¹ Tiyeretseni ife, Ambuye. Tidzadzeni ife mwatsopano ndi Mzimu Woyera. Mulole Mzimu Woyera ungolamulira mmitima mwathu, mwapamwamba, kuti ife tikayende, titaiwala zinthu zomwe ziri m'mbuyo, matope ndi zonyansa zimene ife nthawiina timakhalamo. Ife tikakamira molunjika kukuitana kwa pamwamba, kumene Kuwala kwathu kukhoza kuwala mokoma ndi modzichepetsa, mpaka wodutsa aliyense akhoza kunena kuti, “Uko kuli Mkristu amakhala pa phiri ilo uko. Munthu ameneyo, mkazi ameneyo, bambo ameneyo, ndi duwa lenileni lopatulika la Mulungu. Iwo ndi okoma kwambiri ndi achifundo kwambiri, nthawizonse okonda ndi okoma, ndi omvetsetsa.” Perekani izi, Atate. Mulole ife tikhale a mchere, kuti dziko likhale ndi ludzu; perekani izi, Atate; ndipo tigonjetse zinthu za mdziko lino, ndi zochitika za moyo uno. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Ine ndikhoza. . .

Tsopano tiyeni tingokweza manja athu.

. . . Mpulumutsi. . .

Kuitana chiyani? “Tulukani, muchoke mmatopemo.” Moyo wapamwamba; Chinachake chiri mwa inu, chikukukokerani inu mbali imeneyo. Ndi chiyani chimenecho? Ndi Iyeyo. Pansi mmatope, maluwa aang’ono; inu muli nawo Moyo mmenemo, ukukankhira kwa inu. Ndicho chimene chikukuitanani inu, “Tulukani, muchoke mmatopemo.”

Tsatirani, tsatirani . . .

¹⁹² Tsopano, kodi inu mukutanthauza izo? Tsopano tsekani maso anu.

Komwe Iye anditsogolera ndidzamtsa- . . .

Tsopano dziperekeni nokha. Mutanthauze zimenezo, tsopano.

Komwe Iye anditsogolera ndidzamsatira,
Komwe Iye anditsogolera ndidzamsatira,
Ndinkanaye Iye, Naye, njira yonseyo.

Komwe Iye anditsogolera ine . . .

Basi mokoma tsopano. Kumbukirani, mudziikepo nokha pamenepo.

Iye anditsogolera . . .

“Ine ndiziika izo apa, Ambuye. Ine ndidzakutsatirani Inu, kuyambira tsopano mpakana. Ine ndikuvomereza Izo. Ine ndikukhulupirira Izo.”

Komwe Iye anditsogolera . . .

Kumbukirani, moyo wanu udzachtira umboni mokweza kuposa kamwa lanu. Chimene inu mumakhala chidzatsimikizira kwa anthu mochuluka kuposa chimene inu mukunena.

Ndinka Naye, Naye, (njira, kuti?) njira yonse.

[M’bale Branham akuyamba kung’ung’udza *Komwe Iye Anditsogolera*—Mkonzi.]

¹⁹³ Mungodzipereka nokha, mwakuya, moona mtima, mtima wanu wonse. Bwanji ngati iyi itakhala nthawi yomaliza imene inu mukanalolezedwa kuti mupemphere? Iyo ikhoza kukhala. Ine ndikudalira kuti ayi. Iyo ikhoza kukhala. Ndiye, mukhale otsimikiza tsopano, otsimikiza kwenikweni, otsimikiza kwenikweni. Kumbukirani, chitsekocho chidzatseka, tsiku lina, zikadzatero izo zidzakhala kuti zonse zatha. “Pemphani, inu mudzalandira.”

[M’bale Branham akuyamba kung’ung’udza *Komwe Iye Anditsogolera*—Mkonzi.]

¹⁹⁴ Tangoganizani za ulemelero wonse umene Iye wawupereka kwa inu, chirichonse chimene Iye wachita. “Ine ndikukhulupirira, Ambuye. Ine ndikukhulupirira. Ine ndikukhulupirira kuti Ndinu mgonjetsi wanga. Ine ndikungoyenda ndi Inu, Ambuye. Ine ndikufuna ndikhale

pafupi ndi Inu, kuti komwe Inu muli, kumeneko ine ndikufuna ndikakhaleko.”

¹⁹⁵ Ndipo kumbukirani, Inu munatiuza ife, Atate, kuti, “Ife kwanthawizonse tidzakhala ndi Ambuye, pamene ife tidzakwatulidwe.” Ife tangokhala ndi—tamuwona Iye tsopano, pamene Iye akuyenda ndi ife tsopano. Komano ife tidza... Ndi chinthu chopambana bwanji icho, kungodziwa kuti Iye ali pathu—pakati pathu! Zidzakhala motani pamene ife tidzakhale ndi Iye kwanthawizonse? Ife timakonda kwambiri zochitika zathu zonse: ife tikhoza kupita kokwera; ife tikhoza kupita kokagula; ife tikhoza kupita kokasaka, kowedza, kapena chirichonse chimene ife tingachite posangalala. Koma, oh, akatsegula khomo la tchalitchi, mwaona, ife timafuna kukakomana ndi Ambuye athu. Ndicho chopambana cha zinthu zonse. Ndiye, taganizani, Iye anatonjeza ife. “Ndipo kwanthawizonse kudzakhala ndi Ambuye. Kudzakhala ndi Iye mu mpando Wake, ndi kukakhala ndi Iye kwanthawizonse.” O Mulungu, ife modzichepetsa, ndi—ndi mitu yoweramitsidwa, ife tikuvomereza izo, Ambuye, mu Dzina la Yesu Khristu.

¹⁹⁶ Kodi inu mukumverera kuti inu mukhoza kungochokapo, tsopano, chirichonse, vuto lirilonse? Inu mukhoza kungoyendapo, pamwamba pa ilo tsopano? Ngati inu mukutero, kwezani dzanja lanu, ndikuti, “Mwa chisomo cha Mulungu ine ndikuika yesero ili pansu. Ine sindimenyana nalo ilo, kenanso. Ine ndingowira dzanja Lake, nkuyamba kumayenda.”

“Ine ndamenya, M’bale Branham. Ine ndayesera kuti ndisiye kusuta. Ine—ine ndayesera kusiya tsitsi langa lizikula. Ine ndayesera kuchita *ichi*. Ine ndachita... Ine ndayesera, molimbikira kwambiri, M’bale Branham. Ine ndikulephera basi kuti ndichite izo.”

Musayesere izo, nkomwe. Ingogwirani dzanja Lake, ndikuti, “Atate, Inu muike dzanja langa mu nkono wa malaya.” Mukuona? “Ine ndingokupatsani Inu dzanja langa. Ine ndizingoyenda chitsogolo, Ambuye, ndikuyang’ana kwa Inu.” Izo zichitika. Izo zikuvekani inu ngati Mkhristu weniweni. Inu mukhala Mkhristu weniweni.

¹⁹⁷ Mpaka ine ndidzakuoneni, usikuuno, Mulungu akukondeni inu ndipo akhale ndi inu. Ndinu ana anga a Uthenga. Ndinu ogulidwa.

Tsopano ine ndikuwapereka abusa anu kwa inu, kuti atibalalitse, M’bale Orman Neville.



KODI NDINGAGONJETSE BWANJI? CHA63-0825M
(How Can I Overcome?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marriion Branham unalalikidwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Ogasiti 25, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mu chaka cha ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2018 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org